BUKHU

[LOMASULIRIDWA]

LA

CHIVUMBULUTSO

BUKHU 5
{CHAPUTALA 19 – 22}

Kwa
Mkwatibwi wa Khristu
Bukhu ili laperekedwa

BUKHU {LOMASULIRIDWA} LA CHIVUMBULUTSO

BEN HOWARD

Translated To Chichewa Language

Enoch Kamanula
New Testament Assembly
P.O. Box 64
Mwanza-Malawi

KUSINDIKIZIDWA KOYAMBA 1980

KUSINDIKIZIDWA KACHIWIRI 2005

Palibe gawo la bukhu ili limene lingachulukitsidwe [kupatula lemba la Baibulo] popanda chilolezo cholembedwa. Kuti mumve zambiri lemberani ku:

Sound Of Liberty
Ben Howard
7286 Hwy 53W
Dawsonville, Georgia 30534 (USA)
TwoAnds@soundofliberty.org
www.SoundofLiberty.org

MALONJE

Bukhu la Chivumbulutso ndi bukhu la zoimirira, limene; politanthauzira, ndi uneneri wapamwamba. Iri si bukhu limene likuchita ndi chiphunzitso kapena ziphunzitso za maziko zimene zinabwera kwa ife ndi mtumwi Paulo ndi alembi ena a malemba za m'mene tingapulumutsidwire kapena m'mene tingalandirire dongosolo la chipulumutso la Mulungu.

Bukhu la Chivumbulutso linalembedwa mu 96 A.D. mpingo utagwa ku chikondi chake choyamba. [Chivumbulutso 2:4] Chikuonetsa m'mene mpingo unathera kudutsa mu nthawi mu maonekedwe ake akugwa. Chikuonetsanso [ndipo mofunika kwambiri] mpingo ukubwezeretsedwa ku malo ake a pachiyambi kuno ku nthawi yotsiriza.

Mpingo wapachiyambi sunagwe kuchokera ku bukhu la Chivumbulutso, chifukwa sunali gawo la malangizo wolembedwa kwa mpingo kuchiyambi. Ndi bukhu la mwala wapangodya, ndipo osati bukhu la maziko, ndipo kotero ndilongomasuliridwa kwa mpingo pano pa nthawi yotsiriza. Ndi kalata wa chikondi wa Mulungu kwa mkwatibwi, ndipo Khristu akupanga chikondi ndi mkwatibwi wake pamene Iye akumupatsa iye mzimu wa vumbulutso ndi kuulura zinsinsi kwa iye. Ichi ndi chifukwa cha bukhuli, **"Bukhu [lomasuliridwa] la Chivumbulutso."** Ndi Mulungu kuika Chisomo Chachikulu [Machitidwe 4:33] pa mpingo wake mkwatulo usanachitike.

Komanso, mundirole ndilankhule, kuti owerenga ambiri a bukhu la Chivumbulutso alakwitsa potenga Yohane, mlembi, ngati Yohane nkonzi wa bukhu. Koma palibe njira iriyonse tinganene molondora kuti Yohane ndi nkonzi wa bukhu la Chivumbulutso. Iye anali mlembi, chotengera chabe chimene Mulungu anagwiritsa ntchito kufalitsa malingaliro Ake ku Mau olembedwa kuti awuluridwe pano mu nthawi yotsiriza. Yesu anali, ndipo ndi nkonzi wa bukhu la Chivumbulutso.

Momwemonso olemba bukhu iri akuzindikira mochuluka kuti NKONZI wa bukhu la Chivumbulutso ndi amene wapereka kudzoza kwa kumasulira kwenikweni kwa mlembi uyu. Kotero, ine ndikupemphera kuti mwapemphero inu mutenga kumasulira kwa bukhu la Chivumbulutso chifukwa Mkwatibwi wa Khristu adzamvetsa bwinobwino zimene zikuchitika pano mu nthawi yotsiriza, chifukwa kuwala kwake [kumvetsa] ndi kowala ngati krustalo. [Chivumbulutso 21:11]

Komanso, ndiloreni ndinene ine -Ben Howard- kuti: kwa zaka zoposa 45 ndakhala ndikutumikira pa zolembedwa zimene ziri mu bukhu iri, ngati mishonare mu maiko ambiri ndi kuno ku USA, mu mipingo, maholo, madera, nyumba zobwereketsa, ngati mlaliki wa pa wailesi, kufunsidwa mafunso, ndipo tsopano pa Internet, ngati m'busa wa **Sound of Liberty Assembly** moyandikana ndi Dawsonville, Georgia [USA] ndi mitundu ina ya malo wopezekamo anthu. Mwambiri mwa malo olankhulawa, kufunsidwa mafunso ndi zina, panali kujambulidwa matepi komanso kutenga mfundo zolemba pa zimene zimalankhulidwa zimene ine tsopano sindingathenso kuzilamulira.

- Kotero, zidziwike kwa onse: Kuti bukhu iri lapambana, ndipo laposa, zolembedwa zonse, zojambulidwa kapena mitundu ya nkhani zonse zotengedwa kuchokera kwa mlembi zimene zikuoneka ngati- kapena- zikutsutsana ndi zolembedwa izi, ngati zimenezo zinatengedwa mbuyomu lisanasindikizidwe bukhuli.

- Ichi ine ndikunena, chifukwa maulaliki ambiri pa matepi, ma CD, ma DVD, ma Video, komanso pa Internet apita ku madera ambiri padziko lonse kwa zaka zambiri zimene muli zochepa, ndipo mauthenga ena akale akhoza ngakhale kutsutsa zolemba izi, ine ndachita monga 2 Petro 3:18 amatiphunzitsa ife kuti *"Kukula mu chisomo ndi chizindikiritso cha Ambuye wathu."*

- Kotero, ine ndinena kwa inu kuti ine ndakhala mu utumiki uwu kwa zaka zambiri, monganso inu amene mukuwerenga ichi kwa nthawi yoyamba, kuti bukhu iri lidzapereka kuwala kwakukulu ku "Bukhu la Chivumbulutso" kusiyana ndi mauthenga anga akale amene inu mukhoza kukhala nawo, kaya pa tepi, kulembedwa mwa bukhu, kapena zolemba zanuzanu pa zimene mlembi anapereka, kaya zaka 45 zapitazo kaya zaka 5 zapitazo.

- Ichi ndikunena, chifukwa mzimu womwewo wa Chivumbulutso umene unamupangitsa Yohane kulemba Bukhu la Chivumbulutso wapangitsa kuti limasuliridwe pano mu nthawi yotsiriza kwa Mkwatibwi Wake.

Izi ndikulankhula mokhudzana ndi bukhu lonse la Chivumbulutso, ndipo sirinapangidwe pa cholinga chochotsapo vumbulutso lirilonse limene Mulungu akanapereka patsogolo kwa ine kapena wina aliyense wa atumiki woona wa Mulungu pa Bukhu la Chivumbulutso. Inu mukhoza kukhala otsimikizika kuti vumbulutso lenileni siridzatsutsana ndi zolemba izi.

Posachedwa, utumiki onse woona udzaoneka diso kwa diso [1 Akorinto 1:10] pa kumasulira uku pamene liwu la vumbulutso la Mulungu liyamba kulankhula kuchokera kumwamba mu kufotokoza kwakukulu mwa Mzimu Wake [Chivumbulutso 10:8] pa zinthu zimene mukufuna muwerenge.

Ndikupempheni inu owerenga, kuti muzindikire kuti zolembedwa izi ndi za okhawo amene ali ndi makutu auzimu kuti amve chimene Khristu akunena kwa mkwatibwi wake pamene Iye akupanga chikondi ndi iye, chifukwa Bukhu la Chivumbulutso ndi kalata wa chikondi wa Mulungu kwa Mkwatibwi.

Kotero, mukatha kuwerenga bukhu iri, ngati siringadzutse wamkati wanu ndi kuwalira moyo wanu, ndiye pepani potenga nthawi yanu, ndipo chonde perekani bukhu iri kwa wina aliyense chifukwa chowaganizira mwa pemphero, mwina ndi lawo. Ine ndikukuthokozani mokoma chifukwa cha nthawi yanu ndi mgwirizano.

Pemphero langa kwa inu owerenga ndi iri: *Mulungu akupatseni inu mzimu wa mzeru ndi chidziwitso, ndi kuti maso akumvetsa kwanu awunikiridwe. Kuti mukamvetse masamba otsatira a bukhu iri. Bukhu iri likuthandizeni kuti muvale chovala choyera [Chivumbulutso 19:7-9], kuti musandulike mkazi wa Khristu pokhala m'modzi ndi Mau Ake munthawi yotsiriza iyi. Amen.*

Kuthokoza Kwapadera Kwa …

Ine ndikufunanso ndiwonetsere kuyamikira kwanga pa
ntchito
ya malemu William M.Branham mneneri wa Mulungu
wam'thenga
wa m'badwo uno wa Laodikaya komanso malemu mtumwi
Raymond M. Jackson
amene Mulungu anamugwiritsa ntchito kuti apitirize ntchito Yake imene Iye anaiyamba
kupyolera mwa William Branham; makamaka mu gawo la mbiri la bukhu iri. Ngakhale ife sitiri
othandizidwa, kapena kukwezedwa ndi otsatira a
aliyense
wa uthenga wa amuna amenewa; zolemba zawo zinali zothandiza kwambiri pokonza bukhu iri.

Komanso, kuthokoza kwa padera kwa
-Joyce Howard,
-Gary Gentry,
-Wanda Robertson,
-Barbara Howard,
- Leah Farruggia
ndi Enoch Kamanula
chifukwa cha kuthandiza mosatopa pa ntchito iyi.

"Ndipo anadza m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri akukhala nazo mbale zisanu ndi ziwiri, Nalankhula ndi ine, nanena, Idza kuno, ndidzakuonetsera iwe…" Chivumbulutso 17:1.

Lemba la pamwambali likuonetsa m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri amene akulankhulidwa kudutsa mu bukhu lonse la Chivumbulutso. M'modzi wa iwo akumuonetsa Yohane, amene akuimirira utumiki ngakhalenso kuimirira mkwatibwi, bukhu la Chivumbulutso. Kuona angelo asanu ndi awiri ndi kumvetsa ntchito zawo zimene iwo amachita ndi zinthu zopindula ku kumvetsa kwanu ku bukhu la Chivumbulutso. Izi zatsimikizidwa mu bukhu lonseli ngati chifungulo chenicheni chotsekula zinsinsi za [zoyamba] bukhu lozwizwitsa la Chivumbulutso.
.

MALONJE KU CHAPUTALA CHIRICHONSE

Chaputala cha Khumi ndi Chisanu ndi Chinai

Chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chinai chikuonetsera **anthu akusangalala chifukwa Mulungu waweruza hule wamkulu.** Vesi 7-9 akukamba za Mkwatibwi kuvala bafuta wonyezimira ndipo wakwatiwa ndi Khristu, ndipo ali ku Phwando la Ukwati wa Mwanawankhosa pamene chisautso chikuchitika pa dziko.

Chaputala ichi chikuonetseranso **Khristu ndi Mkwatibwi wake akubwera pa dziko** kudzagwetsa maulamuliro onse ndi mphamvu zonse kumapeto kwa nyengo ya chisautso. Mizimu ya chirombo ndi aneneri abodza yaponyedwa ya moyo mu nyanja ya moto, ndipo otsarira a ankhondo awo anawonongedwa.

Chaputala cha Makumi awiri

Chaputala cha Makumi awiri chikutionetsera ife kuti satana wamangidwa kwa zaka chikwi kumayambiriro kwa mileniamu. Vesi 4 ikutionetsera ife Mkwatibwi pamene akutenga malo ake a ulamuliro kumayambiriro kwa mileniamu. Chikutionetseranso ife kuti oyeramtima a kuchisautso amene anapereka miyoyo yawo chifukwa cha uthenga, pokana kulambira chirombo ndi fano lake, aukitsidwa kwa akufa mu nthawi iyi.

Oyeramtima a kuchisautso apatsidwa malo a ulamuliro mu mileniamu, koma otsika, kusiyana ndi Mkwatibwi.

Chaputala cha makumi awiri chikutionetseranso ife kuti pa nthawi imene ulamuliro wa mileniamu wathu, dziko lidzadzaza ndi anthu amene sanayesedwa. Kotero Mulungu akumasula mdierekezi kwa ka nthawi pang'ono kuti awayese iwo. Satana adzapambana ponyenga chiwerengero chochuluka ngati mchenga wa mphepete mwa nyanja, koma moto unawaononga iwo. Kenako onse akufa adzutsidwa ndi kuwereruzidwa pa mpando waukulu woyera wa chifumu wa chiweruzo, ndipo imfa ndi hade zaponyedwa mu nyanja ya moto kuti zionongedwe. Kenako dziko likupita ku umuyaya.

MALONJE KU CHAPUTALA CHA MAKUMI AWIRI NDI CHIMODZI KOMANSO CHAPUTALA CHA MAKUMI AWIRI NDI CHIWIRI

Ine ndikumverera kuti ndi kofunika kwambiri kuwerenga malonje awa musanayambe kuwerenga machaputala 21 ndi 22. Zikuonetsera dziko likupangidwa latsopano pamene Mulungu akuombola dziko, monga anachitira ndi mtundu wa anthu. Mu machaputala awiri awa, Mulungu akumulora Yohane kuona chimene Iye wachita kudutsa mu nthawi mu dongosolo Lake

la chiwombolo chachikulu. Iye akuonetsera chimene wachita pomulora Yohane kuona Mzimu wake kubweranso ku dziko ku chimene Iye wachiombola. Makamaka chimene Yohane anachiona chikubwera chinali kale pa dziko. Kotero kuti palibe chirichonse chogwirika chimene chikutsika; ndi Mulungu kubwera ku chimene Iye wachiombola. Ndi zabwino motani, pamene tikuona maonekedwe akulu!

Chaputala cha Makumi awiri ndi Chimodzi

Chaputala cha makumi awiri ndi chimodzi chikutionetsera ife kumwamba kwa tsopano, ndi dziko la tsopano zimene olemba ena a malemba analemba za izo. Ndi Munda wa Edeni paliponse pa dziko, kungopatula dera la mamailosi a masikweya 1500 amene ali opambana munda m'mene unaliri. Ndiye mzindawo. Mzindawo sukusowa dzuwa, kapena mwezi kuuwalira iwo. Mpando wa chifumu wa Mulungu ndi Mwanawankhosa ndiye kuwala kwa malo awa kumene oyeramtima oyera a ulemerero amakhala, chimene ndi mzinda, koma zimatengera dzuwa ndi mwezi kuwalira kotsarira kwa dziko kumene mafuko akhalako. [Yesaya 30:26]

Chaputla cha makumi awiri ndi chimodzi chikuonetsera kumwamba kwa tsopano ndi dziko latsopano, ndi kunja kwa mzinda wa Mulungu; zimene zikuphatikiza zipata, linga ndi maziko; kubwera ku dziko latsopano ndi kufotokoza kunja kwa mzinda.

Chaputala cha Makumi awiri ndi Chiwiri

Chaputala cha makumi awiri ndi chiwiri chikutionetsera ife **mkati mwa mzinda;** mpando wa chifumu, mtsinje wa moyo, mtengo wa moyo ndi zipatso zache zosiyanasiyana khumi ndi ziwiri. Masamba a mtengo uwu wa moyo ndi machiritso kwa mafuko a anthu. Pa nthawi iyi, palibenso themberero, palibenso imfa, palibe chirichonse koma madalitso ndi chimwemwe cha Ambuye, pamene tikhala ndi Iye amene anatiombola mu umuyaya onse.

Mulungu akudalitseni pamene mukuwerenga bukhu iri ndi pemphero langa.

Mu Dzina la Yesu Khristu,

M'bale Ben Howard

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHA KHUMI NDI CHISANU NDI CHINAI

Vesi lotsiriza la chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chitatu likuti, *"Ndipo momwemo munapezedwa mwazi wa aneneri ndi oyera mtima, ndi onse amene anaphedwa padziko."* Ndi chimene chinapezeka mu Babulo, mu kachitidwe aka ka chipembedzo, ndipo Mulungu anatsanulira chiweruzo Chake pa iye. Koma apa, mu chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chinai, tikubwerera ku maonekedwe a kumwamba. Yohane ali mu masomphenya ake.

Vesi 1: *"Zitatha izi ndinamva ngati mau akuru a khamu lalikulu m'mwamba, liri kunena, Aleluya; chipulumutso, ndi ulemerero, ndi mphamvu, nza Mulungu wathu."*

Taonani kumene izi ziri: Masomphenya a Yohane anabwereranso kumwamba. Iye anaona anthu ambiri akulemekeza Mulungu. Winawake akhoza kunena kuti ndi chinthu choipa kuona nkhondo yaikulu, chionongeko chachikulu, ndi kuona mpingo waukulu ukuonongeka, koma mwa iye munapezeka mwazi wa oyeramtima. Iye ndi wakupha. **Kumwamba kunayamba kusangalala pamene utsi wa kupsa kwake unakwera kumwamba, chifukwa Mulungu anamuweruza iye pa zimene anachita**.

Vesi 2: *"Pakuti maweruzo ache ali woona ndi olungama; ndipo anaweruza mkazi wa chigololo wankuru, amene anaipsa dziko ndi chigololo chake, ndipo anabwezera chilango mwazi wa akapolo ache pa dzanja lache la mkaziyo."*

Apa akuti, *"Ndipo anaweruza mkazi wa chigololo wankuru."* Kodi Iye akumuweruza liti? Iye akumuweruza iye kumapeto kwa sabata la 70 la Danieli. Apa pali maonekedwe akumwamba pamene akulemekeza Mulungu ndi kumuuza Iye kuti wachita chinthu cholondora, ndi kuti maweruzo Ache ali woona. Kodi mumadziwa kuti mumalemekeza Mulungu polankhula kuti, "Ambuye, mukuchita chinthu cholondora, maweruzo anu ndi woona." Ine ndikukhulupirira kuti pa zokhudza ntchito ya Ambuye Iye akuchita chinthu cholondora, sichoncho? Ife tikuona gulu iri la Laodikaya uyu likudulidwa, ndipo mipingo ikuzirara. Ife tikhoza kunena, "Mulungu mukuchita chinthu cholondora pochotsa Mzimu ndi kuuyika mwa Mkwatibwi." Kumeneko ndi kulemekeza Mulungu. Taonani zimene amachita. Iwo amazindikira chilungamo cha Mulungu mu machitidwe ake. Ine ndikufuna inu muone zimenezo.

Inde, oyeramtima akulemekeza Mulungu chifukwa Iye akuweruza hule wamkuru amene anadetsa dziko lapansi ndi chigololo chake, ndipo wabwezera mwazi wa akapolo Ake pa dzanja lache.

Vesi 3: *"Ndipo anatinso, Aleluya. Ndipo utsi wake unakwera ku nthawi za nthawi."*

Taonani kuti utsi wa hule wakaleyo wa mu mzinda wa Vatican ukukwera kumwamba, ndipo okhala kumwamba akuona ndipo akulemekeza Mulungu ndi kunena kuti maweruzo ache ndi woona.

Vesi 4*: "Ndipo anagwa pansi akuluwo makumi awiri mphambu anai ndi zamoyo zinai, ndipo zinalambira Mulungu wakukhala pa mpando wa chifumu, nizinena, Amen; Aleluya."*

Vesi 5: *"Ndipo mau anachokera ku mpando wa chifumu, ndi kunena, Lemekezani Mulungu wathu akapolo ache onse, akumuopa Iye, ang'ono ndi akulu."*

Vesi 6: *"Ndipo ndinamva ngati mau a khamu lalikulu, ngati mkokomo wa madzi ambiri, ngati mau a mabingu alimba, nizinena, Aleluya; pakuti achita ufumu Ambuye Mulungu wathu, Wamphamvuyonse."*

Ine ndikufuna kuti muone kuti gawo loyamba la chaputala ichi, kudutsa mu vesi 6, ndi kulemekeza Mulungu, ndi kuzindikira chimene Iye wachita. Akuti, *"Ambuye Mulungu wathu alamulira."* Ndi Mulungu kutenga ulamuliro wa zochitika. Anthu akumulemekeza Iye chifukwa cha zimene Iye akuchita.

Tsopano, zonse ziri m'malo mwake kuti Ambuye abwere ku dziko kudzalamulira. Pamene ndinena "Ambuye" apa, ndikulankhula za mamuna Yesu Khristu kubweranso kudzakhala Mfumu, koma ine ndikufna inu muone kuti maonekedwe awa asanafike a Yesu kubwera ku dziko ngati Mfumu, akuonetsera ukwati utachitika ndipo Yesu wakwatira Mkwatibwi. **Mfundo yakuti Mkwatibwi akubweranso ndi Khristu zikutanthauza chinthu chimodzi, iye wakwatulidwa kuchoka ku dziko. Iye wakwatulidwa nyengo ya chisautso chachikulu chisanayambe**.

Taonani m'mene aliri amgwiro Mau a Mulungu, ndi m'mene Mulungu waziikira apa molondora. Chifukwa ngati ife titangopitirira kulankhula za hule, ndikumangopitirira kulankhula za Khristu kubwera ndi Mkwatibwi, ndipo palibe malo a Mkwatibwi kutengedwa, ndiye tikhoza kudzifunsa tokha, "Kodi Mkwatibwi anakwatulidwa liti?" Taonani, zikuonetsera iye kukwatiwa ndi Iye. Inu mukukwatiwa mwa uzimu ndi Iye mwa vumbulutso la Mau a Mulungu, pamene mukulandira Mau amenewo mu mtima mwanu.

Vesi 7: *"Tikondwere, tisekerere, ndipo tipatse ulemerero kwa Iye, pakuti wadza ukwati wa Mwanawankhosa; ndipo mkazi wache wadzikonzekera."*

Pakuti mkuru akumuuza Yohane kuti asekere, zikutanthauza kuti ife tikhale okondwa ndi osangalalanso. Taonani, vesi lachisanu ndi chiwiri likumutchula iye "mkazi Wache." **Iye wasandulika m'modzi ndi Khristu.** [Aefeso 5:31-32]

Vesi 8: *"Ndipo anampatsa iye abvale bafuta onyezimira woti mbu; pakuti bafuta ndiye zolungama za oyeramtima."*

"Ndipo anampatsa Iye," kutanthauza kuti zachitika kale pa nthawi imene Yohane akuziona izi, chifukwa amaona izi mu tsiku lathu.

Vesi 9: *"Ndipo ananena ndi ine, Lemba, Odala iwo amene aitanidwa ku phwando la ukwati wa Mwanawankhosa. Ndipo ananena ndi ine, Iwo ndiwo mau owona a Mulungu."*

Kodi mukuona kuti ukwati wachitika kale? Mkwatibwi watengedwa kale pa dziko pa nthawi iyi. Khristu mwa Mzimu wake watulutsa Mkwatibwi. Ine ndikufuna kuti muone chimene iye wabvala, chifukwa ine ndikufuna kugwiritsa ntchito mau omwewo mu vesi lina mu chaputala ichi. **Iye anabvala bafuta onyezimira, wonyezimira woti mbu.** Izi zikuzindikiritsa gulu lina la anthu, ndipo iwo ndi Mkwatibwi wa Khristu. Mu masiku a Baibulo, bafuta wonyezimira chinali chovala chapamwamba chimene mukanatha kugula.

Mu chaputala cha chisanu ndi chiwiri cha bukhu iri, kodi iwo anali ndi chiyani amene anatuluka mu chisautso chachikulu? Iwo anali ndi minjiro yoyera. Kodi Ayuda pansi pa chisindikizo chachisanu amene anaphedwa ndi Hitler anabvala chiyani? Iwo anapatsidwa minjiro yoyera. Taonani kuti kagulu aka sikanapatsidwe mwinjiro yoyera, koma iwo abvala zapamwamba zimene ndalama ikhoza kugula, tikhoza kunena motero. Kodi mukufuna kuti mubvale mu chapamwamba chimene Mulungu ali nacho? Ndiye tengani chilungamo cha Mulungu polandira Mau a Mulungu.

Vesi 10: *"Ndipo ndinagwa pa mapazi ache kumlambira iye. Ndipo ananena ndi ine, Tapenya, usatero; ine ndine kapolo mzako, ndi mnzao wa abale ako akukhala nao umboni wa Yesu; lambira Mulungu: pakuti umboni wa Yesu; ndiwo Mzimu wa chinenero."*

Kodi mkuru uyu ndi ndani amene Yohane akumulambira? Tiyeni titsegule ku Chivumbulutso 7. Ine ndikufuna kukuonetsani ichi chifukwa lakhala liri funso. Ine ndikufuna kukuonetserani amene amaonetsa Yohane zinthu izi kuyamba ndi kuyamba. Akuru makumi awiri mphambu anai ndi zamoyo zinai mu chaputala cha chisanu ndi chiwiri ndi omwewo amene alembedwa mu chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chinai.

M'modzi mwa akuru amenewa anabwera kwa Yohane. Chivumbulutso 7:13-14- *"Ndipo m'modzi wa akuru anayankha, nanena ndi ine, Iwo abvala zobvala zoyera ndiwo ayani, ndipo achokera kuti? Ndipo ndinati kwa iye, Mbuye wanga, mudziwa ndinu. Ndipo anati kwa ine, Iwo ndiwo akutuluka m'chisautso chachikulu; ndipo anatsuka minjiro yawo, naziyeretsa m'mwazi wa Mwanawankhosa."* Awa ndi oyeramtima a kuchisautso mu chaputala chachisanu ndi chiwiri. **Koma chimene ndikufuna kuti muone ndi ndani amene amalankhula ndi Yohane.** Ndani amene amamuonetsa Yohane chimene vumbulutso la izi limatanthauza? Anali ndani? M'modzi mwa akuru makumi awiri mphambu anai. Iye anamuonetsa iye oyeramtima aku chisautso. Kenako, ndi mkuru yemweyo amene anamuonetsa iye Mkwatibwi. Siwina ayi. Taonani m'mene Mau a Mulungu amadziyankhira okha. Awa ndi akuru khumi ndi awiri ndi atumwi khumi ndi awiri a Mwanawankhosa. Mu chaputala chachinai cha Chivumbulutso, Yohane anatengedwa kumwamba kumene iwo anali atakhala mozungulira mpando wa chifumu, ndipo mu chaputala cha chisanu, m'modzi mwa akuru anayamba kulankhula ndi Yohane mu masomphenya ake. Pamene mu zochitika zenizeni, Yohane anali m'modzi mwa akuru, koma kumbukirani kuti awa ndi masomphenya.

Mu chaputala ichi cha khumi ndi chisanu ndi chinai cha Bukhu la Chivumbulutso, Yohane anagwa kulambira mkuru uyu. Ife tikhoza kuona chifukwa chake pamene tiwerenga ku chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chiwiri, vesi lachitatu, kuti *"m'modzi wa angelo asanu ndi awiri"* anamutenga Yohane mu Mzimu ndi kumufotokozera za hule wankulu, ndi zina, ndipo mu chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chinai iye anauzidwa za Mkwatibwi wa Khristu. **Mngelo anamutenga iye kupita naye m'masomphenya a vumbulutso awa, koma anali mkuru amene amafotokoza.** Kodi mukuona zimene zinachitika? Komanso, mu zenizeni Yohane mwiniwake anali mkuru, koma Mulungu sanamulore iye kuziona mu njira imeneyo, chifukwa sizinali zoti zichitike mu tsiku la Yohane. Mkuru uyu pa chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chinai anati, "Ine ndiri ngati iwe, kapolo mzako." Tithokoze Ambuye kuti mkuru uyu sanavomereze kulambiridwa kuchokera kwa Yohane, kapolo mzake. Iye akhale chitsanzo chathu.

Vesi 11: *"Ndipo ndinaona mutatseguka m'Mwamba; ndipo taonani, kavalo woyera, ndi Iye wakumkwera wotchedwa Wokhulupirika ndi Woona; ndipo aweruza, nachita nkhondo molungama."*

Kodi chingakhale chiyani *"kumwamba kutseguka?"* Tiyeni tiringalire za zimenezi mwa kanthawi pang'ono. Ndi chomwecho chimene chisindikizo cha chisanu ndi chimodzi chikuonetsera- pamene dzuwa linada ngati chithumba ndi nyenyezi zinagwa kuchokera kumwamba, ndi kuwala konse kwa kumwamba kunachotsedwa. Kumwamba kunafutukuka ngati bukhu lofunyulura m'mene lifunyidwa. Chinali chiyani? Mulungu akuchotsa kuwala konse

kumene kumakhudza dziko. Kuwala kokhako kumene kunaliko, kunali kuzungulira kubwera kwa Ambuye pamene Iye akubweranso ku dziko. Dzuwa lasiya kuwala. Dziko likudutsa mu nthawi yaikulu ya mavuto. Pali chivomerezi ndi matalala. Izi zaonetsedwa pansi pa chisindikizo chachisanu ndi chimodzi ndi muliri wa chisanu ndi chiwiri. Ndi zonse izi zochitika, mukhoza kuganiza ndi nthawi yovuta yotani komanso nthawi yotani ya chisokonekero. Kenako Mulungu akubwera ndi kuchotsa kuwala kwa kumwamba. Ndi pamene anthu amakhala ndi mantha. Kenako Mulungu akuchita chinachake. Mulungu akulora chochitika ichi kutha maora 24, mochuluka moti dziko likhoza kuzungulira kamodzi kukwaniritsa Chivumbulutso 1:7 kumene *"diso liri lonse lidzamuona Iye."*

Mu m'dima uwu onse, kukakhala m'dima ochuluka, kanthawi kamodzi kumwamba kwatseguka ndipo apo pakubwera Yesu ndi Mkwatibwi kubweranso ku dziko. Apo pakubwera Yesu ndi kudziko ndi iye amene Iye amene anamukwatula chisautso chisanayambe. Apo pakubwera Yesu ku dziko pamodzi ndi amene wakwatira ngati mkazi wake. Ndi Khristu ndi mkazi wake kubweranso ku dziko. Pamene iwo akutsika, anthu akuruakuru a pa dziko, mafumu a padziko, a msinga ndi mfulu akuthamangira ku matanthwe ndi mapiri ndi kufuula, *"Tigwereni, ndikutibisa pa nkhope ya Iye amene akhala pa mpando wa chifumu, ndi mkwiyo wa Mwanawankhosa."* Ichi ndi chisindikizo cha chisanu ndi chimodzi; koma Yohane anachiona icho apa mu maonekedwe amene sanawaonepo. Chifukwa chiyani? Apa chinachake chaonjezeredwa. Ndi chiyani? Ndi Khristu ndi mkazi wake. Taonani tikuwerenga chinthu chomwecho ku Mateyu 24, mu chaputala 6, 11, ndi 16 cha Chivumbulutso; koma pamene tibwera ku chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chinai cha Chivumbulutso, Khristu pamodzi ndi mkazi wake akubwera pa dziko.

Vesi 12: *"Ndipo maso ake ali ngati lawi lamoto, ndi pamutu pake pali nduwira zachifumu zambiri; ndipo ali nalo dzina lolembedwa; wosalidziwa wina yense koma Iye yekha."*

Iye akubweranso kudzaweruza ndikudzachita nkhondo. Pa mutu pake pali nduwira zambiri. Awa ndi masomphenya. Kodi nduwira zochuluka zikutanthauza chiyani? Nduwira imaimirira mfumu pa mafuko kapena anthu**. Pa chifukwa choti Yesu anabwera ndi nduwira zambiri zikutanthauza kuti Iye akubwera kudzatenga ufumu wina uli wonse, ndi boma lirilonse pa nkhope ya dziko.** Sikuti iye akubwera ndi nduwira zenizeni zitaphatikidwa pa mutu pake, koma Yohane anaona Iye ali ndi nduwira zambiri, kusonyeza kuti Iye akudzatenga ndikulamulira maboma onse a dziko lapansi. Iye adzakhala olamulira pa maufumu onse.

Ku Bukhu la Danieli 7:18 akuti- *"Koma opatulika a Mwambamwamba adzalandira ufumuwo, ndi kukhala nao ufumu kosatha, ku nthawi zonka muyaya."* Kodi ndi chiyani? Yesu Khristu, Mfumu ya mafumu, ndi Mbuye wa ambuye, kubwera kudzatenga, ndipo pamene Iye atenga akumulora mkazi wake, mfumukazi Yake, kulamulira pamodzi ndi Iye.

Vesi 13: *"Ndipo abvala chovala chowazidwa mwazi; ndipo atchedwa dzina lache, Mau a Mulungu."*

Kodi mukudziwa chimene Mau a Mulungu ali? Yohane 1:1- *"Pachiyambi panali Mau ndipo Mau anali kwa Mulungu, ndipo Mau ndiye Mulungu."* Yohane 1:14 akuti, *"Ndipo Mau anasandulika thupi, nakhazikika pakati pathu, [ndipo tinaona ulemerero wake, ulemerero wonga wa obadwa yekha wa Atate,] odzala ndi chisomo ndi choonadi."* Kodi zimenezo zikufotokoza chimene Iye ali? Ndi Mau a Mulungu kukhala munthu mwa Yesu Khristu, kapena Mau kusandulika thupi, kubweranso ku dziko. **Iyi ndi nthawi yoyamba imene akumuonetsa Iye ndi**

atavala chovala cha mtundu uwu. Chavikidwa mu mwazi. Iye sikuti akukwatira. Iye wakwatira kale pamene izi zikuchitika. Sikuti sanavale chovala cha ukwati Chake, koma wavala chovala Chake cha ukwati ndipo akupita kukamenya nkhondo, ndi kukagwetsa adani ake. Iye wavala chovala ndipo chavikidwa mu mwazi, kutanthauza kuti pakhala kukhetsa mwazi. Iye akubwera ku dziko ndipo adzagwetsa maulamuliro onse a thupi, ndi auzimu, ndi maulamuliro onse.

Vesi 14: *"Ndipo magulu ankhondo okhala m'mwamba anatsata Iye, okwera pa kavalo oyera, obvala bafuta woyera woti mbu."*

Apo pakubwera Mkwatibwi. Kodi akavalo oyera ndi chiyani? Ndi mphamvu ya Mau. Taonaninso awa amene akubwera pamodzi ndi Iye m'mene abvalira. Iwo abvala bafuta woyera woti mbu. Pali gulu limodzi lokha lobvala bafuta woti mbu, woyera. Ameneyo ndiye mkazi wake. *"Ndipo mkazi wake wadzikonzekera. Ndipo anampatsa iye abvale bafuta wonyezimira woti mbu."* Kodi mukuona amene akubwera pamodzi ndi Iye? Ndi Mkwatibwi, amene watengedwa chisautso chisanakhale, kubweranso kudzathandiza kugwetsa adani. Ndi chimodzimodzi mamuna ndi mkazi pamene akwatirana. Iwo amapita nyumba, pali zambiri m'menemo zimene sakuzikonda. Kotero iwo amalowa nyumba ndi kukhala ndi kukonza kwabwino. M'bale padzakhala kukonza kwa nyumba. Pamene Yesu ndi Mkwatibwi atsiriza, adzasandulika malo a ukhondo.

Vesi 15: *"Ndipo mkamwa mwache mutuluka lupanga la kuthwa, kuti akanthe nayo mitundu ya anthu; ndipo Iye adzawalamulira ndi ndodo ya chitsulo: ndipo aponda Iye moponderamo mphesa mwa vinyo waukali wa mkwiyo wa Mulungu wa Wamphamvuyonse."*

Vesi 16: *"Ndipo ali nalo pa chovala chake ndi pa ntchafu yake dzina lolembedwa, MFUMU YA MAFUMU, NDI MBUYE WA AMBUYE."*

Kodi lupanga lakuthwa ndi chiyani? Ndi Mau. Zikutanthauza kuti akulankhula kuti Iye akulankhula Mau a chiweruzo. Kodi chinachitika ndi chiyani ndi iwo ku chaputala cha khumi ndi chinai cha Zakariya amene anabwera kutsutsana ndi Yerusalemu? Baibulo likuti anathedwa atangoima pa mapazi awo. Ngakhale maso awo anasungunuka mkati mwao. Ndi Mau olankhulidwa a Mulungu a chiweruzo.

Kodi mukuona chimene chikuchitika? Ndi Yesu Khristu kubweranso ku dziko ndi Mkwatibwi wake. Kumbukirani m'mene ku chaputala cha khumi ndi chinai cha Chivumbulutso, Iye anamasula mphamvu zimenezi kutuluka kukasonkhanitsa mafuko onse ku nkhondo ya Armageddon; ndipo mngelo anaponya zenga lache pa dziko, kusonkhanitsa zipatso, ndikuziika moponderamo mphesa? Chabwino, izo zangochitika mu masomphenya awa amene Yohane adawaona. Kenako mwamsanga, Yesu akubwera kudzatsiriza ntchito yogwetsa adani Ake, nyanga khumi ndi anzake.

Mu gawo loyamba la chaputala ichi, pali kusangalala kumene kukuchitika kumwamba chifukwa hule akuweruzidwa. **Pamene chisangalaro ichi chikupitirira kumwamba, mafumu khumi amene anaononga chirombo hule ali otanganidwa kufulumizitsa ankhondo kuwabweretsa pamodzi ndi kulowa mudera la Yerusalemu. Pakadali pano Kutali Kum'mawa, anthu onse a chi Oriental ali ndi mtundu wao wa chikomunisti, ndipo akufulumizitsa ankhondo ndi kuwabweretsa ku Chigwa cha Megiddo, zamphamvu ma milioni mazana awiri. Nkhondo yaikulu ikuyambika; ndipo mafuko khumi a ku Ulaya akugonjetsa ma Orientals. Pa nthawi yomweyo nyanga khumi zikutenga ndi kuyamba**

kulamulira, apa pali chimene chikuchitika: Zivomerezi zonse zikuchitika, kumwamba kukuchita m'dima, ndipo apo pakubwera Ambuye Yesu Khristu ndi Mkwatibwi pamodzi ndi Iye. Mafuko khumi amenewo akonzeka kale atabvala za nkhondo ndipo akuyamba kumenyana ndi Mbuye wa ambuye ndi Mfumu ya mafumu, Yesu Khristu. Kodi mukuona m'mene zidzakhalire pamene Iye akubwera ku dziko? Tiyeni tiwerenge Chivumbulutso 17:14- *"Iwo adzachita nkhondo pa Mwanawankhosa, ndipo Mwanawankhosa adzawalaka, chifukwa ali Mbuye wa ambuye, ndi Mfumu ya mafumu; ndipo adzawalakanso iwo akukhala naye, oitanidwa, ndi osankhika ndi okhulupirika."* Nyanga khumi zimenezo zikutembenuka ndikuchita nkhondo ndi Ambuye Yesu Khristu ndi Mkwatibwi; ndipo pa nthawi imeneyo iwo akuonongedwa.

Vesi 17: *"Ndipo ndinaona mngelo ali kuima m'dzuwa; ndipo anafuula ndi mau akulu akunena ndi mbalame zonse zakuuluka pakati pa mlengalenga: Idzani kuno, sonkhanitsani ku phwando la Mulungu wamkuru."*

Vesi 18: *"Kuti mukadye nyama ya mafumu, ndi nyama ya akapitao, ndi nyama ya anthu amphamvu, ndi nyama ya akavalo, ndi ya iwo akukwerapo, ndi nyama ya anthu onse, mfulu ndi akapolo, ang'ono ndi akulu."*

Vesi 19: *"Ndipo ndinaona chirombocho, ndi mafumu a dziko, ndi magulu a nkhondo awo, osonkhanitsidwa kuchita nkhondo pa Iye wakukwera pa kavalo, ndi gulu la nkhondo lache."*

Vesi 20: *"Ndipo chinagwidwa chirombocho, ndi pamodzi nacho m'neneri wonyenga amene adachita zizindikiro pamaso pache, zimene anasokeretsa nazo iwo amene adalandira lemba la chirombo, ndi iwo akulambira fano lache; iwo awiri anaponyedwa ali moyo m'nyanja ya moto yakutentha ndi sulfure."*

Taonani kuti pali maphwando awiri mu chaputala ichi: Phwando la Ukwati la Mwanawankhosa, ndi Phwando la Mulungu wankulu. Pa phwando la Ukwati wa Mwanawankhosa, tikulandira mphamvu ya kulamulira ndi Khristu. Iwo a ku Phwando la Mulungu Wamkulu akudyedwa ndi mbalame za mlengalenga. Tsopano mukudziwa phwando loti mukakhalepo.

Chionongeko chachikulu ichi chikuchitika pamene Yesu akubweranso pa dziko kudzagwetsa adani ake. Zikatha izi, pali dongosolo latsopano pa dziko. Ngati inu mutati muime pamenepo, inu simukanaona mngelo ataima pa dzuwa, ndipo inu simukanamva mau akulankhulidwa kwa mbalame za mlengalenga, "Bwerani ndipo mudzisonkhanitse nokha pamodzi." Koma kulora chinachake kufa, inu simukusoweka ku kumva mau. Muziyang'ane mbalame zam'madzi; zidzayamba kusambira. Inu mukakamba za chivundi Pakati Kum'mawa; anthu mamilioni mazana awiri anafa mu nkhondo. Yohane anaziona izo ngati kulankhula kwa mbalame zamlengalenga kuti *"bwerani ndi kuzisonkhanitsa nokha."* Padzakhala zikwizikwi za mbalame zimene zidzabwera, chifukwa Mulungu akukonzekera kuzidyetsa phwando lalikulu. Fungo lidzabweretsa mbalame zimenezi.

Pamene ankhondo adzakwapulidwa, kodi Khristu akuchita chiyani chotsatira? Iye akubwera kufika ndi kutenga mzimu wa kachitidwe ka chirombo, ndi kufikira ndi kutenga mzimu wa kachitidwe ka otsutsakhristu, ndiye muone chimene akuchita nao. *"Onse awa anaponyedwa amoyo mu nyanja ya moto yoyaka ndi sulfure."* Chaponyedwa m'menemo ndi chiyani? Mizimu iwiri imeneyo, **ndipo pamene chirichonse chiponyedwa mu nyanja ya moto sichitulukanso.** Chifukwa chiyani chaponyedwa m'menemo? Chaponyedwa m'menemo ku chionongeko

chathunthu. Sungani mu malingaliro anu kuti awa ndi anali masomphenya amene Yohane adawaona, ndipo panalibe munthu amene anaponyedwa m'menemo. Panalibe chirombo chimene chinaponyedwa m'menemo chokhala ndi mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi, koma inu mukanakhala Yohane mutaima pamenepo kuyang'ana pa izo, ndi zimene mukadaona; koma kutanthauzira kwa izo sikumeneko. Kutanthauzira kwa izo ndi uku: Mizimu imene inayambitsa kachitidwe aka pa dziko idzachotsedwa kwa nthawizonse pa nthawi iyi.

Vesi 21: *"Ndipo otsalawa anaphedwa ndi lupanga la Iye wakukwera pa kavalo, ndilo lotuluka m'kamwa mwache; ndipo mbalame zonse zinakhuta ndi nyama zao."*

Adani agwetsedwa. Mizimu ya otsutsakhristu ndi chirombo yaponyedwa mu nyanja ya moto. Otsalira a ankhondo akudyedwa ndi mbalame za mlengalenga, ndipo Khristu akukonzekera kuika Ufumu Wake pa dziko. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHA MAKUMI AWIRI

Ife taona mu chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chinai cha bukhu iri kumene nkhondo ya Armageddoni inachitika ndipo Yesu anabwerera ku dziko. Iye anagwetsa ulamuliro onse ndi maukuru. **Chaputala cha makumi awiri chikuonetsera nyengo ya zaka chikwi kumene m'dierekezi wamangidwa, keneko iye wamasulidwanso patatha zaka chikwi.**

Vesi 1: *"Ndipo ndinaona mngelo anatsika Kumwamba, nakhala nacho chifungulo cha phompho, ndi unyolo waukulu m'dzanja lache."*

Vesi 2: *"Ndipo anagwira chinjoka, njoka yakaleyo, ndiye m'direkezi ndi satana, nam'manga iye zaka chikwi."*

Vesi 3: *"Namponya ku phompho, natsekapo, nasindikizapo chizindikiro pamwamba pache, kuti asanyengenso amitundu kufikira kudzatha zaka chikwi; patsogolo pache ayenera kumasulidwa kanthawi."*

Choyambirira, Yohane adaona Ambuye akubwera ku dziko kumapeto kwa m'bado, kudzathetsa nkhondo zonse. Taona chirombo ndi aneneri onyenga akuponyedwa mu nyanja ya moto, koma satana iyemwini waponyedwa mu dzenje la phompho. Yohane anaziona izi mu masomphenya, ngati mngelo wamkulu kubwera ndi chingwe chachikulu, ndi kumumanga satana kwa zaka chikwi. Dziko likusintha ulamuliro apa. Yesu Khristu akuyamba ulamuliro Wake, ndipo pali dongosolo lina likubweretsedwamo. Uku ndikuyamba kwa ulamuliro wa mileniamu.

Vesi 4: *"Ndipo ndinaona mipando ya chifumu, ndipo anakhala pamenepo; ndipo anawapatsa chiweruziro; ndipo ndinaona mizimu ya iwo amene adawadula khosi chifukwa cha umboni wa Yesu, ndi chifukwa cha Mau a Mulungu, ndi iwo amene sanalambire chirombo, kapena fano lache, nisanalandira lembalo pamphumi ndi dzanja lao; ndipo anakhala ndi moyo, nachita ufumu pamodzi ndi Khristu zaka chikwi."*

Ngakhale anamwali opusa a Amitundu, ndi oyeramtima aku chisautso, ndi oyeramtima a Chiyuda amene aphedwa chifukwa cha Mau a Mulungu adzaukitsidwa kwa kufa kumayambiriro kwa ulamuliro wa mileniamu. Mkwatibwi oyeramtima adzazindikira ulamuliro umene adzalamulira. *"Ndipo ndinaona mipando ya chifumu, ndipo anakhala*

pamenepo; ndipo anawapatsa chiweruzo." Anapatsidwa m'manja mwawo kuweruza ngati mkazi wa Khristu. Ndi Mkwatibwi oyeramtima pamene akutenga malo ake.

Inde, chiwerengero ichi chimene chadzutsidwa ndikupatsidwa moyo wamuyaya kumayambiriro kwa mileniamu ndi gulu ilo la anthu limene linali lokhulupirika ku Mau a Mulungu, kukhulupirika kwa Yesu Khristu, koma sanaukitsidwe kwa kufa kufikira kumayambiriro kwa mileniamu. Oyeramtima awa ndi okhulupirika kwa Mulungu ndipo anakana kulambira otsutsakhristu.

Iwo amene akukhala pa mipando ya chifumu sanaweruzidwe, koma kwapatsidwa kwa iwo kuweruza. Kodi iwo aweruza chiyani? Choyambirira, iwo ndi oti athandize kuweruza iwo amene anapereka miyoyo yawo chifukwa cha Mulungu Mkwatulo utachitika. Kenako, athandiza kuweruza anthu amene adzakhale mu mileniamu. Komanso kwapatsidwa kwa iwo kusunga chinthu ichi molunjika kudutsa mu nthawi yonse ya mileniamu.

Kumbukirani kuti mu chaputala cha chitatu cha Chivumbulutso, vesi 21, Yesu anati, *"Iye wakulakika, ndidzampatsa akhale pansi ndi Ine pa mpando wa chifumu wanga, monga Inenso ndinalakika , ndipo ndinakhala pansi ndi Atate wanga pa mpando wachifumu wache."* Ndiloreni ndifotokoze monga chonchi. Siziri ngati m'mene mungadzukire ndikunena kwa Yesu, *"Kwenikweni, Yesu, ine ndikufuna kukhala nawe pamodzi pa mpando."* Ayi, mpando wachifumu ndi malo a ulamuliro. Kotero Mkwatibwi adzagawana udindo wa ulamuliro; monga Baibulo likunena, Iye adzapanga olamulira ena olamulira mizinda isanu, ena kulamulira mizinda iwiri, ndi zina zotero. Zimatengera ndi m'mene mwakhalira okhulupirika ku Mau a Mulungu mu moyo uno. Malo anu mu mileniamu zidzatengera m'mene mwakhalira okhulupirika ku chimene Mulungu wakuitanirani kuti muchite. Iye amene akhulupirika ku zazing'ono ndi okhulupirika ku zambiri. Iye amene sangakhulupirike ku zazing'ono ndi osakhulupirika ku zazikulu. Mulungu adzaziyanga moteromo.

Pali magawo atatu a chiukutsiro choyamba. Ife tikufuna kutulutsa oyeramtima onse ku manda kumayambiro kwa mileniamu. Sipadzatsala china chiri chonse mu dziko chimene chiri ndi moyo osatha mu ulamuliro wa mileniamu. Ndiloreni ndilankhulenso ichi, ndipo ine ndikufuna inu mukhale okhazikika ndi kuchigwira ichi. Palibe chirichonse chimene chiri ndi moyo wamuyaya chimene chidzakhale chakufa mu ulamuliro wa zaka chikwi wa mileniamu. **Palibe chirichonse chimene chidzauka mu chikukitsiro cha chiwiri chimene chidzapatsidwa moyo wa muyaya. Chirichonse chimene chiri ndi moyo wa muyaya chidzauka mu chiukitsiro choyamba.** Taonani apa, kuti pali zaka chikwi pakati pa chiukitsiro choyamba ndi chachiwiri.

Kodi gawo loyamba la chiukitsiro linachitika liti? Linachitika pamene Yesu Khristu anapachikidwa ndi kuukanso. Iye anafa ndikutsikira kupita pa mtima wa dziko, kukalalikira ku mizimu ya ku ndende, kumasula a msinga, ndikutulutsa oyeramtima onse a ku Chipangano Chakale amene amayembekezera kudza kwa Messia. Izi zikuphatikiza Abrahamu, Isake, Yakobo, ndi oyeramtima onse aku Chipangano Chakale.

Ine ndikufuna ndiwerenge Mateyu 27: 51-53 ndi kukuonetserani ichi. *"Ndipo onani, chinsalu chotchinga cha m'kachisi chinan'gambika pakati, kuchokera kumwamba kufikira pansi; ndipo dziko linagwedezeka, ndi miyala inang'ambika; ndi manda anatseguka, ndi mitembo yambiri ya oyeramtima, akugona kale, inauka; ndipo anatuluka m'manda mwao pambuyo pa kuuka kwache, nalowa m'mzinda woyera, naonekera kwa anthu ambiri."* Kodi mukuona chiukitsiro cha

oyeramtima aku Chipangano Chakale? Yesu anapita ku nyumba ya ndende ya satana, ndipo chinthu choyamba chimene anachita ndi kutenga zifungulo ku mbali ya satana. Iye anatsekula ndende ndikulora Abraham, Isake, ndi Yakobo, ndi oyeramtuima onse aku Chipangano Chakale kutuluka. Chimene chinachitika kwa iwo ndi chiyani? Iwo anaonekera amoyo. Iwo anapita mu mzinda wa Yerusalemu ndi kuonekera kwa ambiri. Pamene Iye anatsikira ku paradaizo, Iye anawatengera ku malo a mpumulo, mtendere, ndi chimwemwe kuyembekezera nthawi imene onse oyeramtima abweranso ku dziko. Kotero inu mukuona kuti chiukitsiro chimodzi chachitika kale. Pali "chiukitsiro chimodzi" chokha koma pali magawo atatu a icho.

Taonani kuti gawo limodzi la chiukitsiro choyamba lachitika kale. Mu nthawi ya Paulo, anthu anafika posokonezeka ndipo anayamba kumufunsa Paulo zokhudza zinthu izi. Iye analemba kalata nthawi ina ndikuwauza kuti asavutike ndi zinthu izi, chifukwa iye awauza yankho lenireni kuchokera kwa Mulungu.

Ku 1 Atesalonika 4:13-16, Paulo akulankhula za chiukitsiro Mkwatibwi oyeramtima. *"Koma sindifuna, abale, kuti mukhale osadziwa za iwo akugona; kuti mungalingalire monganso otsalawo, amene alibe chiyembekezo. Pakuti ngati tikhulupirira kuti Yesu adamwalira, nauka, koteronso Mulungu adzatenga pamodzi ndi Iye iwo akugona mwa Yesu. Pakuti ichi tinena kwa inu m'mau a Ambuye, kuti iye wokhala ndi moyo, otsalira kufikira kufikanso kwa Ambuye, sitidzawatsogolera ogonawo. Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka."* Apa pali chinachake chimene sichinalembedwepo kufikira nthawi iyi imene Paulo amalankhula. Kodi mungaganizire munthu kuima ndikuyamba kulankhula zinthu ngati zimenezo? **Ndi udindo wa utumwi umene ukulankhula.** 1 Atesalonika 4: 17-18- *"Pamenepo ife otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse. Chomwecho, tonthozanani ndi mau awa."*

Tiyeni tiwerenge zinanso pa ichi ku 1 Akorinto 15:51-52. Pakamwa pa mboni ziwiri kapena zitatu mau onse akhale okhazikika. *"Taonani, ndikuuzani chinsinsi; sitidzagona tonse, koma tonse tidzasandulika, m'kamphindi, m'kutwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza; pakuti lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osabvunda, ndipo ife tidzasandulika."* Paulo anati, *"Taonani ndikuuzani chinsinsi."* Kenako akulankhula za anthu amoyo kusandulika, ndi anthu akufa kuukitsidwa. **Ndi gawo lachiwiri la chiukitsiro.** Kodi izi zikuchitika liti? Izi zikuchitika pa nthawi imene Ambuye akubweranso kudzatenga oyeramtima amoyo. Taonani, kuti akufa akuukitsidwa koyamba. Kenako ife amene tiri ndi moyo ndi otsala tikukwatulidwa kukakumana ndi Ambuye mu mlengalenga; apa ndi pa mkwatulo. Izi zikupanga Mkwatibwi oyeramtima. Iri ndi gawo lachiwiri la chiukitsiro.

Ku Chivumbulutso 20:4, Yohane anaona iwo amene anaphedwa chifukwa cha Mau chifukwa cha umboni wa Yesu, amene sanalandire chilemba cha chirombo kapena kupembedza fano lache; amayenera kukhala oyeramtima aku chisautso. Nthawi yokhayo imene chirombo chidzalankhula ndikukakamiza anthu kulambira chirombo ndi fano lache, ndi mugawo lotsiriza la sabata la 70 la Danieli.

Baibulo likuti mu gawo lotsiriza la vesi la 4 *"ndipo anakhala ndi moyo, nachita ufumu pamodzi ndi Khristu kwa zaka chikwi,"* zimene zinapanga gawo lachitatu la chiukitsiro choyamba. Zimenezo zinatulutsa chirichonse chimene chikanakhala ndi moyo wamuyaya chimene chinali chakufa. Sipadzakhala aliyense woukitsidwa kumapeto kwa ulamuliro wa

mileniamu ndi kupatsidwa moyo wa muyaya. Zonse zimene ziri ndi moyo wa muyaya zabweretsedwa apa pa Chivumbulutso chaputala 20:4.

Taonani, chonde, magawo atatu a chiukitsiro choyamba. Oyeramtima aku Chipangano Chakale anauka pamene Yesu anauka. [Mateyu 27:51-53] Mkwatibwi oyeramtima adzauka oyeramtima okhala ndi moyo asanasandulike ndipo Mkwatulo ukuchitika. [1Akorinto 15:51-55, ndi 1 Atesalonika 4:17-18] Oyeramtima aku chisautso ndi akufa ena amene aikizidwa ku moyo wamuyaya adzauka chisautso chitatha, pamodzi ndi Mkwatibwi oyeramtima ndipo adzakhala ndi moyo ndi kulamulira ndi Khristu kwa zaka chikwi, ngakhale kuti ndi mphamvu zochepa. Ine ndikupemphera kuti muzione izi.

Vesi 5: *"Otsala a akufa sanakhalenso ndi moyo kufikira kudzatha kwa zaka chikwi. Ndiko kuuka kwa akufa koyamba."*

Tsopano, taonani chiukitsiro choyamba ichi. Pamene oyeramtima a ku Chipangano Chakale anauka kwa akufa Yesu atauka, inali *gawo loyamba* la chiukitsiro choyamba. *Gawo lachiwiri* ndi pamene Mkwatibwi oyeramtima akuukitsidwa. *Gawo lachitatu* ndi pamene oyeramtima a kuchisautso akuukitsidwa, ndi ena onse amene ali ndi moyo. Zimenezo zikutsiriza chiukitsiro choyamba. Kodi mukuziona izo? Paulo anati akufa adzaukitsidwa, koma munthu aliyense mu dongosolo lake.

Vesi 6: *"Wodala ndi oyeramtima ali iye amene achita nao pa kuuka koyamba; pa iwowa imfa ya chiwiri iribe ulamuliro; komatu adzakhala amsembe a Mulungu ndi a Khristu, nadzachita ufumu pamodzi ndi Iye zaka chikwizo."*

Taonani apa akuti, *"Wodala ndi oyeramtima ali iye amene achita nao pa kuuka koyamba,"* kapena amene ali ndi gawo mu zimenezo; posayang'anira kuti ndi oyeramtima a ku Chipangano Chakale, Mkwatibwi wa oyeramtima, oyeramtima aku chisautso, kapena Ayuda amene anaphedwa chifukwa cha Mau a Mulungu. Iwo adalitsika ngati angakhale ndi gawo la chiukitsiro choyamba pakuti *"pa iwowa imfa ya chiwiri iribe ulamuliro."*

Tsopano, kodi imfa yachiwiri ndi chiyani? Ife tikudziwa chimene imfa yoyamba iri. Ndi pamene tisiya kupuma, pamene mtima usiya kupopa magazi, ndi pamene palibe moyo mu thupi iri. Inu mumati, "Mamuna ameneyo kapena mkazi ameneyo wamwalira." Apa zikukamba za imfa yachiwiri. **Iwo amene akuikitsidwa mileniamu isanayambe, imfa yachiwiri iribe mphamvu pa iwo.** Imfa yachiwiri ndi imfa ya munthu wamkati. Munthu wamkati ndi opangidwa ndi moyo ndi mzimu ndipo zimenezo inu simungazione. Munthu wakunja ndi wopangidwa ndi thupi. Pamene munthu wakunja amwalira ife tikhoza kuwona izo ndipo timadziwa chimene chikuchitika. Iwo amaikidwa m'manda. Ife timawaika iwo mu nthaka ndi kuwakwirira. Pamene munthu wamkati amwalira, zikutanthauza kuti mzimu ndi moyo wa munthu ameneyo wasweka, ndikupita komweko kumene unali usanakhale moyo- utatha kuotchedwa mu nyanja ya moto. **Mzimu umabwerera kwa Mulungu amene anaupereka; gawo lokhalo la Mulungu limene linapangitsa moyo kuti ukhale wamoyo, ndi chokhacho chimene chimabwerera kwa Mulungu amene anapereka iwo.** [Mlaliki 12:7] Koma chikhalidwe cha uchimo chimene mzimu umatengera ngati munthu, waonongedwa mu nyanja ya moto. Ndi moyo wa munthu umene umatayika. Ichi ndi chimene Baibulo limaphunzitsa, kotero zimazipanga kukhala zolondora. Apo pali pamene anthu amasokonezera ndi kuganizira kuti hade ndi wamuyaya. Palibe chinthu ngati hade wa muyaya. Imfa yachiwiri imaononga ngakhale wokhala mkati wamunthu. Kodi mukuziona izo? Imfa yoyamba ndi imfa ya thupi. Ndiye kenako

pali imfa yachiwiri, koma ngati muli ndi gawo mu chiukitsiro choyamba, inu simukuyenera kuopa imfa yachiwiri. Imfa ndi hade zaponyedwa mu nyanja ya moto, monga tidzaona kutsogolo kwa chaputala ichi.

Tisanasiyane nacho ichi, ine ndikufuna kuti ndikhale otsimikizika kuti mukumvetsa chaputala cha makumi awiri cha Bukhu la Chivumbulutso kudutsa mpakana mu vesi 6. Choyambirira Ambuye akubwera, kutenga Ufumu wache, ndi kumanga m'dierekezi. Kenako, Mkwatibwi oyeramtima akutenga malo awo. Oyeramtima akuukitsidwa kwa kufa, aliyense amene ali ndi moyo wa muyaya. Iwo ali padziko lino onse tsopano, kukhala moyo ndi kulamulira pamodzi ndi Khristu kwa zaka chikwi osaopa imfa. Awa ndi anthu awa owukitsidwa. Satana wamangidwa mu zaka chikwi izi, ndipo zonse zikuyenda bwinobwino kwa zaka chikwi.

Vesi 7: *"Ndipo pamene zidzatha zaka chikwi, adzamasulidwa satana m'ndende yache."*

Pali mafuko a anthu amene adzalowa mu ulamuliro wa mu mileniamu wa Khristu ngati anthu kudzachulukana pa dziko. Pa nthawi imene nyengo iyi ya zaka chikwi ikutha, dziko lidzakhala litachulukana ndi anthu. Kumayamambiriro kwa nthawi iyi, kudzakhala dongosolo latsopano. Padzakhala ufumu watsopano. Zonse zachitika mosiyana ndi kale. Kenako pakatha zaka chikwi, dziko lidzakhala ngati munda wa Edeni. Aliyense ndi okondwa, koma mwadzidzi chinachake chikuyamba kuchitika kwa anthu kuthupi. Adzayamba kuyesedwa. Satana wamasulidwa ku ndende yake kukayesa anthu nyengo iyi ya zaka chikwi ikatha.

Anthu adzayamba kuchita mantha, kapena chiri chonse chimene chidzachitike pa nthawi imeneyo. Satana adzamasulidwa ku ndende yake kudzayesa iwo, kudzaona kuti ndi ndani amene adzalemekeza ulamuliro wa Mulungu mu nthawi imeneyo. Sipadzakhala mpingo wina wa kachitidwe kabodza, sikudzakhala kachitidwe kakale kachirombo ka Chiroma. Adzakhala mayesero a anthu kuona ngati ali okhulupirika kwa Mulungu, kapena adzamvera mayesero a satana.

Kumbukirani kuti Mkwatibwi ndi amene adzakhala ndi ulamuliro. Satana nthawi zonse wakhala akufuna ulamuliro, ndipo wakhala akuyesera kugwetsa pansi ulamuliro wa Mulungu, kulikonse kumene ulamuliro uli. Kumbukirani kuti Mulungu anaikiza mwa iye ulamuliro mu nthawi imene mbiri isanayambe, koma iye sanathe kuzilemekeza izo. Kudutsa mu njira yonseyi, satana wayesera kugwetsa ulamuliro wa Mulungu, dongosolo la Mulungu ndi zina zotero. Pamene adzamasulidwanso, iye sadzasintha kachitidwe kake. Iye adzagwiritsa njira zosiyanasiyana. Chidzakhala chinthu chomwecho, kuyesera kugwetsa chimene Mulungu waika. Zikatha zaka chikwi, iye adzapita kukayesa anthu.

Vesi 8: *"Nadzatuluka kudzasokeretsa Amitundu ali mu ngodya zinai zadziko, Gogo, ndi Magogo, kudzawasonkhanitsa achite nkhondo: chiwerengero chawo cha iwo amene chinakhala ngati mchenga wa kunyanja."*

Pali mau amodzi mu vesi lachisanu ndi chitatu limene ine ndikufuna kuti muligwiritsitse, chifukwa mu machaputala awiri otsatirawa mudzaona kufunika kwake. Mau amenewo ndi "mafuko." Padzakhala mafuko amene adzalowa mu m'bado wa muyaya ngati gawo la oyera mtima.

Apa kuti *"chiwerengero chawo cha iwo amene chinakhala ngati mchenga wa kunyanja."* Kodi anthu onse awa anachokera kuti? Kodi iwo anaukitsidwa kapena chinachake? Ayi. Anali ana amene anabadwa mwa anthu amene anapita mu mileniamu pamene iwo amakula, iwo amapitirira kuchulukana monga anachitira chitatha chigumula mpakana padzakhala,

mosakaikira, mamilioni a wanthu pa dziko. Padzakhala anthu okwanira odzatchedwa “mafuko.” Mkwatibwi adzakhala akulamulira ndipo satana adzamasulidwa ku ndende. Iye adzapita kukanyenga mafuko amenewa, ndipo adzapambana ponyenga chiwerengero chachikulu ngati mchenga wa ku nyanja, ndi kuwasonkhanitsa kukonzekera nkhondo yotsutsana ndi ulamuliro wa Mulungu. Kodi ulamuliro wa Mulungu udzakhala kuti? Kukhazikika mu Yerusalemu koma mwa anthu oyeramtima pa dziko lonse lapansi. Oyeramtima adzatenga ufumu.

Vesi 9: *“Ndipo anakwera nafalikira m’dziko, nazinga tsasa la oyeramtima ndi mudzi wokondedwawo: ndipo unatsika moto wakumwamba nuwanyeketsa.”*

Oyera mtima sadzayenera kumenya nkhondo ina akangofika mu mileniamu. Taonani ichi. Nkhondo ya Armaggedoni ndi nkhondo yotsiriza imene mtundu wa anthu adzamenyapo. Kenako chidzachitika ndi chiyani ku mapeto kwa mileniamu pamene mdierekezi akusonkhanitsa anthu awa pamodzi ku nkhondo ya oyeramtima? Nthawi yomweyo akadzangokonzekera nkhondo pa anthu oyeramtima a Mulungu, pa nthawi yomweyo imene satana akonzeka kupanga kusuntha kwake kotsiriza motsutsana ndi dongosolo la Mulungu, kodi mukudziwa chimene chidzachitika? Moto udzachokera kumwamba ndi kudzapha anthu. Udzawapha iwo adakali chiimire pa mapazi awo. Ndi chimene chidzachitike kwa anthu amenewa. Ndi kumapeto kwa mileniamu. Izo zikusiya padziko, mafuko a wanthu amene sadzalambira mdierekezi. Zikusiya pa dziko anthu, dongosolo la oyeramtima. Inu mudzaona kufunika kwa izi mu machaputala awiri otsatirawa. Sidongosolo la oyeramtima aku Chipangano Chakale. **Si dongosolo la oyera mtima a ku Chipangano Chatsopano, koma ndi dongosolo limene likutchedwa mafuko.** Mafuko amenewa adzabweretsa ulemerero wao ndi ulemu wawo mu mzinda. Mulungu amafuna dongosolo pamene iye amamulenga Iye mwana ndikumutcha dzina lache Adamu. Iye amafuna dongosolo, mafuko a wanthu amene akanadzakhala ndi moyo wamuyaya mu gawo la thupi. Milemiamu itatha, Iye adzakhala nawo. Kenako nthawi idzaima, zonse zidzapita ku ungwiro, ndipo m’bado uwo wamuyaya udzayamba kuyenda. Kodi mukuona mafuko mu mileniamu? Mafuko omwewa amene ali mu mileniamu adzapita mu m’bado wa muyaya ngati anthu mu thupi, koma moto ukugwa kuchokera kumwamba ndi kuononga iwo amene ananyengedwa ndi mdierekezi, ndi kumenyana ndi dongosolo la Mulungu.

Vesi 10: *“Ndipo mdierekezi wakuwasokeretsa anaponyedwa m’nyanja ya moto ndi sulfure, kumeneko kulinso chirombocho ndi mneneri wonyengayo; ndipo adzazunzidwa usana ndi usiku ku nthawi za nthawi.”* [Satana adzazunzidwa kumene aneneri onyenga ali ndi kuwaonongedwa kumapeto kwake.]

Vesi 11: *“Ndipo ndinaona, mpando wa chifumu waukulu woyera, ndi Iye wakukhalapo, amene dziko ndi m’mwamba zinathawa pamaso pake, ndipo sanapezedwa malo awo.”*

Yohane akuona zonse za zinthu izi, kuona chiukitsiro, kuona mileniamu, kuona mdierekezi kumangidwa, kuona moto ukugwa, ndipo **kenako mwadzidzi chirichonse chazimira mu masomphenya a Yohane kupatula mpando wa chifumu.** Iye amayang’ana pa dziko ndi kuona chirichonse, ndipo onse a iwo amaoneka ngati kubwerera mbuyo, apo panali iye ali kuyang’ana pa mpando wa woyera wachifumu ndi Iye wakukhala pa mpando woyera waukulu wa chifumu.

Kodi kumwamba ndi dziko zinapita? Kodi chirichonse chinapita ndipo panalibe chirichonse chotsala koma mpando wa chifumu? Ayi. Mu masomphenya a Yohane chirichonse chinapita, ndipo chonse amaona chinali mpando wa chifumu woyera waukulu. Kunali kutsimikiza pa chimene chikuchitika, chifukwa patsogolo pake mu chaputala ichi, nyanja inapereka akufa.

Dziko lidakali pompano, nyanja ikadali pompano, Yohane adakali pompano, Mkwatibwi adakali pompano, oyeramtima adakali pompano, mafuko adakali pompano, ndipo dzikolapansi likupita ku muyaya.

Iye, amene akhala pa mpando wa chifumu apa ngati Oweruza ndi Yesu Khristu. Ichi ndi chinthu chotsiriza chimene Iye adzachita. Kenako Iye adzapereka ulamuliro kwa Mulungu, malingana ndi 1 Akorinto 15:24 pamene Iye asiya ulamuliro ndi mphamvu zonse, kenako mwa mwiniyekha adzamvera Atate wake, ndipo Mulungu adzakhala Mulungu, zonse mu zonse. Inde, Yesu Khristu akukhala apo ngati oweruza ndi mphamvu ya Mulungu wa muyaya zoikidwa mwa Iye; **chifukwa mu zenizeni zake Mulungu sanasamutsiribe likuru lake ku dziko.** Awa ndi masomphenya amene Yohane anali nawo, ndipo pamene Yohane anaona iwo, iye anadziwa kuti munthu amene wakhala pa mpando anali ndi ulamuliro wonse wa Mulungu kuseli kwa Iye pamene Iye apereka chiweruzo. Iye anali nawo ulamuliro onse wa Mzimu wa Muyaya.

Vesi 12: *"Ndipo ndinaona akufa, akulu ndi ang'ono alikuima pa mpando wa chifumu; ndipo mabukhu anatsegulidwa, ndipo bukhu lina linatsegulidwa, ndilo la moyo; ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m'mabukhu, monga mwa ntchito zawo."*

Vesi 13: *"Ndipo nyanja inapereka akufawo anali momwemo, ndipo imfa ndi hade zinapereka akufawo anali m'menemo; ndipo anaweruzidwa yense monga mwa ntchito zake."*

Vesi 14: *"Ndipo imfa ndi hade zinaponyedwa m'nyanja yamoto. Iyo ndiyo imfa yachiwiri, ndiyo nyanja ya moto."*

Vesi 15: *"Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m'bukhu la moyo, anaponyedwa m'nyanja yamoto."*

Bukhu iri la moyo latsegulidwa chifukwa cha anthu athupi amene ali ndi moyo padziko.

Tiyeni tione kufunika kwa bukhu la moyo pamene likutsegulidwa, pamene masomphenya a Yohane amapereka malingaliro a Mulungu kwa ife. **Zikuonetsera kwa iwo amene apulumutsidwa, amene maina awo anali mu bukhu la moyo maziko a dziko la pansi asanakhale, ndi kuti ali gawo la banja la Mulungu.** Iwo anali odziwidwiratu a Mulungu ndi kuikidwiratu kukhala fanizo la mwana wache, Yesu Khristu. [Aroma 8:28-30] Izi zikukhudza anthu ku thupi amene adzapita mu mileniamu ngati anthu mu thupi, komanso anthu amene anthu amene adzabadwa mu nthawi ya mileniamu amene adzakhalabe mu maonekedwe a thupi. Oyeramtima awa [anthu ku thupi] akudziwika ngati, "mafuko" kapena "mafuko a iwo opulumutsidwa" ku Chivumbulutso chaputala 21 ndi 22. Maina awo adzakhala momwemo mu bukhu. Oyeramtima awa sadzalandira matupi a ulemerero; iwo adzakhala nthawi zonse mu maonekedwe a thupi, koma ndi kukhala ndi moyo wamuyaya.

Mabukhu ena anali a zochitika kuonetsera iwo amene anaponyedwa mu nyanja ya moto; chifukwa chiyani anaponyedwa m'menemo, ndi kudziwa ndimochuluka bwanji aliyense angaotchedwere. Yohane adaona izi ngati kuti kunali mabukhu enieni, koma mu zenizeni ziri mu malingaliro a Mulungu.

Akufa onse amene aukitsidwa apa, akuweruzidwa monga mwa ntchito zawo. Zatchulidwa kuti *"mabukhu anatsegulidwa: ndipo bukhu lina linatsegulidwa, limene ndi bukhu la moyo."* Mu zenizeni zake, palibe bukhu pa malopo, inu mukhoza kunena. Chifukwa chiyani? Chifukwa Mulungu ndi Mzimu ndipo Iye alibe kumwamba kodzala ndi mabukhu ndi zosungiramo mabukhu. Iye akafuna kupeza chirichonse chokhudza aliyense wa ife, Iye sakuyenera kupeza mlembi kuti ayang'ane m'mabukhu, ndi kuyang'ana maina athu, ndikuona zimene tachita. Iye

anadziwiratu ngakhale dziko lisanakhale chirichonse chimene tingadzachite ndi lingaliro liri lonse limene tingadzalingalirire. Kotero chifukwa chiyani Iye akanafuna kuzilemba izo mu bukhu? Kotero anthu aukitsidwe ndi kuweruzidwa malingana ndi ntchito zawo. Mulungu akudziwa. Iye amaika muyezo wa chiweruzo umene uli woyenera ndi iwo. Kenako akuwaponya iwo mu nyanja ya moto. **Palibe chirichonse chimene chiri ndi moyo wa muyaya chimene chidzaukitsidwa kwa kufa mu chiukitsiro cha chiwiri.**

Vesi 13 likutulutsa matupi onse akufa kuchokera ku nyanja, matupi onse akufa kutuluka mu dziko, ndi mizimu yonse kutuluka mu hade. Gwirani vesi 13; ikuonetsa kuti imfa ndi hade zidzapereka zonse ziri mwa iwo. Kenako imfa ndi hade zaponyedwa mu nyanja ya moto.

Kodi mukudziwa kuti kuli anthu oterowo lero amene akutchedwa "mizimu ya ziwanda" amene ndi angelo akugwa? Iwo akuweruzidwanso, kuponyedwa mu nyanja ya moto, ndi kuonongedwa; pamodzi ndi anthu akugwa onse. Akuti, "Imfa *ndi hade* zinapereka akufa anali m'menemo." Taonani kusiyana. Pamene akuonetsera *imfa* akutanthauza anthu amene anakhala pa nkhope ya dziko. Koma pamene akuti *hade,* akutanthauza mizimu yonse ya ziwanda ndi mizimu yonse yoipa imene iri pa nkhope ya dziko tsopano, imene yakhala iripo kudutsa mu nthawi yonse. **Ndi mdierekezi yekha amene akuponyedwa mu nyanja ya moto pamene moto ukugwa, koma pamene hade akupereka akufa, akuperekanso ziwanda zonse zimene zinamangidwa mu hade.** Iwo adzatuluka ndi kuima pamaso pa Yesu Khristu kuweruza. Chifukwa chiyani? Chifukwa pa ma masiku amene iwo amayesedwa, anali ndi kusankha. Panali Mikayeli, mngelo wankulu, ndi Gabrieli, mngelo wina wapadera, amene anakhala woona kwa Mulungu ngakhale pamene Lucifala anagwa. Magawo awiri a magawo atatu a angelo a Mulungu anakhala moona ndipo sanamvere satana. Angelo amenewo amene anagwa mu m'bado wa Adamu adzayenera kuima pa mpando wa chifumu oyera wachiweruzo uwu, koma osati ngati anthu, chifukwa iwo sanali anthu kuyamba ndi kuyamba; koma ngati angelo akugwa. Chinthu chonsecho chidzaponyedwa mu nyanja ya moto ndi kuonongedwa. Kenako chimene Mulungu adzachita chiyani? Iye adzaononga angelo onse akugwa, ndi anthu onse akugwa. Vesi 15 ikuti, aliyense amene dzina lache sirinalembedwe mu bukhu la Mwanawankhosa wa moyo anaponyedwa mu nyanja ya moto. Vesi 14 ikuti, *"Ndipo imfa ndi hade zinaponyedwa m'nyanja yamoto. Iyo ndiyo imfa yachiwiri."* Kodi zimenezo zinachita chiyani? Zinamuononga satana, ntchito zache zonse, ndi mtundu onse wa anthu amene anaukira motsutsana naye Mulungu. Kenako Mulungu anachita chiyani? Iye anachotsa matupi akufa onse mu nyanja, matupi onse akufa ku dziko, ndi kukuyeretsa dziko ku mizimu yoipa yonse. Palimodzi zidzayaka munyanja ya moto mpakana Mulungu atakhutitsidwa, pamene dziko likupita ku umuyaya. Pa nthawi iyi, mu nthawi ya kusintha iyi, nthawi idzaima ndipo umuyaya ukuyamba pamene Yesu akupereka ufumu kubwerera ku Mzimu wa Muyaya.

Tiyeni tiwerenge 1 Akorinto15: 24- *"Pomwepo pali chimaliziro, pamene adzapereka ufumu kwa Mulungu, ndiye Atate, atatha kuthera chiweruzo chonse, ndi ulamuliro wonse, ndi mphamvu yomwe."* Pamene akuti, *"Pomwepo pali chimaliziro,"* zikukamba za kumapeto kwa mileniamu, kapena pamene nthawi ifika kumathero. 1 Akorinto 15:25- *"Pakuti ayenera kuchita ufumu kufikira ataika adani onse pansi pa mapazi ache."* Izi zikukamba za Yesu. Munthu Khristu Yesu akuyenera kulamulira pa dziko mpakana Iye atagwetsa adani onse. Kenako ndi chiyani achite**? Iye akutenga ufumu kupitanso kwa Mulungu, ngakhale Atate.** "Yesu Yekhayo" anthu samatha kumvetsa izi, sichoncho?

Ine ndikufuna muone m'mene izi zikuchitikira. Izi zikuchitika chiweruzo cha mpando wachifumu woyera chitatha. Ichi ndi chinthu chotsiriza chimene chaikidwa m'manja mwa Yesu. Iye akukhala pamenepo ngati oweruza. Iye akuweruza onse amene anakhala pa nkhope ya dziko. Dziko ndi nyanja zikupereka akufa awo ndipo akuponyedwa mu nyanja ya moto. Iye wagwetsa ulamuliro onse ndi maukuru onse, ndipo chiweruzo chokaphedwa chachotsedwa. Padzakhala nthawi imene chiweruzo chokaphedwa chidzatha; ndi nthawi imene m'dani wotsiriza adzaonongedwa, ndi m'dani otsiriza ameneyi ndi imfa.

Tiyeni tiwerenge kotsatira kwa 1 Akorinto. Chiweruzo chokaphedwa chathedwa ndipo Yesu akulamurira mpakana Iye akugwetsa adani ake onse. 1Akorinto 15:26-28- *"M'dani wotsiriza amene adzathedwa ndiye imfa. Pakuti iye anagonjetsa zonse pansi pa mapazi ache. Koma pamene anena kuti zonse zagonjetsedwa, kuzindikirika kuti sawerengerapo Iye amene anagonjetsa zonsezo kwa Iye. Ndipo pamene zonsezo zagonjetsedwa kwa Iye, pomwepo Mwana yemwe adzagonjetsedwa kwa Iye amene anagonjetsera zinthu zonse, kuti Mulungu akhale zonse mu zonse."* Kodi mukuona kusintha kukuchitika?

Kumapeto kwa mileniamu, pamene tifika ku m'bado wa Muyaya uwu, Yesu Khristu watsiriza kubweretsamo banja la Mulungu, ndi pamene ife tikhala olowa pamodzi ndi Khristu. Baibulo likuti ku Aroma kuti ife tiri *"olowa ndi Mulungu komanso pamodzi ndi Khristu."* Mwakulankhula kwina, Yesu Khristu ndi woyamba wobadwa wa Atate, ndipo Mwana woyamba wobadwa akutenga zonse za Atate. Kodi Yesu akuchita chiyani pamene Iye akutenga zonse za Atate? Iye akuzigawa izo kwa onse woomboledwa. Inde, Iye akuzigawa zonse ndi banja la Mulungu. **Kenako Yesu Khristu mwiniwake akupereka mphamvu ndi ulamuliro zimene zinaikizidwa mwa Iye kwa Mulungu, Atate, ndipo Mulungu akukhala zonse mu zonse.** Kenako Mulungu akukonzanso pamwamba pa dziko. Kenako Yohane akuona masomphenya akupita mu m'bado wa muyaya ndi dziko latsopano. Amen.

MALONJE KU CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHAMAKUMI AWIRI NDI CHIMODZI KOMANSO MAKUMI AWIRI NDI CHIWIRI

Mu vesi loyamba la Chivumbulutso, chaputala makumi awiri ndi chimodzi, Yohane akuona dziko pamene likulowa mu umuyaya, apa ndi pamene latuluka mu mileniamu, Khristu watsiriza ntchito Yache ndipo wabwezeretsa ufumu kwa Atate. [1 Akorinto 15:24-28] Tsopano pali dziko latsopano, ndipo ndi m'mene Mulungu anaziikira kuti zikhale kuyambira pachiyambi.

Mu vesi lachiwiri, Yohane akuona mzinda, Yerusalemu Watsopano, ndipo ndi mzinda wa uzimu, monga m'mene mudzaphunzirira pamene muwerenga machaputala awiri otsatirawa a bukhu iri. Nditalankhula zimenezo, tiyeni tiwerenge 1 Akorinto 2:7-16; *"Koma tilankhula nzeru ya Mulungu m'chisinsi, yobisikayo, imene Mulungu anaikiratu, pasanakhale nyengo za pansi pano, ku ulemerero wathu, imene saidziwa m'modzi wa akulu a nthawi ya pansi pano: pakuti akadadziwa sakadapachika Mbuye wa ulemerero; koma monga kunalembedwa, zimene diso sirinaziona, ndi khutu sirinazimva, nisizinalowa mu mtima wa munthu, zimene ziri zonse*

Mulungu anakonzeratu iwo akunkonda Iye. Koma kwa ife Mulungu anationetsera izi mwa Mzimu; pakuti Mzimu asanthula zonse, zakuya za Mulungu zomwe. Pakuti ndani wa anthu adziwa za munthu, koma mzimu wa munthuyu uli mwa iye? Momwemonso za Mulungu palibe wina adziwa, koma Mzimu wa Mulungu. Koma sitinalandira ife mzimu wa dziko lapansi, koma Mzimu wa kwa Mulungu, kuti tikadziwe zimene zinapatsidwa kwa ife ndi Mulungu kwaufulu. Zimenezonso tilankhula, si mau ophunzitsidwa ndi nzeru za munthu, koma ophunzitsidwa ndi Mzimu; ndi kulinganiza zamzimu ndi zamzimu. Koma munthu wa chibadwidwe cha umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu: pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, chifukwa ziyesedwa mwauzimu. Koma iye amene ali wauzimu ayesa zonse, koma iye yekha sayesedwa ndi m'modzi yense. Pakuti wadziwa mtima wa Ambuye, kuti akamlangize Iye? Koma ife tiri nawo mtima wa Khristu."

Mu chaputala 21 ndi 22, tikuona mofulumira lingaliro la Mulungu ku chimene Iye anali nacho mu malingaliro mu M'munda wa Edeni; kulengera mtundu wa anthu malo a mwambamwamba kukhala pano padziko. Iye amafunanso mamuna ndi mkazi, amene anawalenga kumukonda ndi kumukondetsetsa Iye ndi chikondi chenicheni, pamene akanabveka ndi kusunga dziko.

Kotero m'malo moti mtundu wa anthu umukonde ndi kumukondetsetsa Mulungu ndi chikondi chenicheni, ndiye pamayenera kukhala chisankho. Kotero, Mulungu anapatsa Adamu ndi Hava mitengo yonse yobereka ndipo iwo amaikonda, ndipo anali osangalala. Koma kuti awapatse iwo kusankha, Mulungu anaikanso mitengo ina iwiri (malamulo) mu munda wa Edeni, ndi kuitcha Mtengo wa Moyo ndi Mtengo wa kudziwa zabwino ndi zoipa. Mitengo imeneyi (malamulo) imayenera kuchita ndi langizo la Mulungu ku Genesis, chaputala choyamba chimene chinati, "Kuchulukana ndi kuligonjetsa kapena kudzaza dziko."

Ku Genesis, chaputala 1:31; **Mulungu anaona zonse zimene Iye anapanga, ndipo zinali zabwino…, zimenezo zimaphatikiza serpent, ndipo zimaphatikizanso Mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa.** Chinthu chokhacho chimene Mulungu adaona chimene sichinali chabwino, chinali kuti munthu [Adamu] akhale yekha, opanda nzache. Kotero analenga omuthandizira [Hava] kukhala mkazi wache. [Genesis 2:18-25]

Ambuye Mulungu anaika Mtengo wa Chidziwitso mu munda, kuti iwo akathe kukakhala ndi moyo mwa nzeru **ngati atasankha.** Mtengo wa Chidziwitso unali wabwino kwambiri pamene umagwiritsidwa ntchito pamodzi ndi Mtengo wa Moyo. Pamene Mtengo wa Moyo unalumikizidwa pamodzi ndi Mtengo wa Chidziwitso, ukanatha kubereka ana; ana akazi ndi amuna okhala ndi moyo wamuyaya. Koma kuti akampatse Adamu ndi Hava kuyesa ngati akanatha kusunga Mau Ake, Mulungu anamuloranso serpenti amene anampereka kukhala wantchito kwa Adamu ndi Hava, kudzozedwa ndi mdierekezi kuyesa ana Ake, ngati akanatha kudikira mu nthawi ya Mulungu kubwera palimodzi kubereka ana, kapena kumvera serpenti ndi kudya za mu Mtengo wa Chidziwitso mosalumikizana ndi Mtengo wa Moyo.

Kutenga za mitengo yonse iwiri mwa chifuniro cha Mulungu, chikanakhala Adamu ndi Hava kubwera palimodzi ndi madalitso a Mulungu mu kulumikizana kwao pamodzi zimene anaziikiza kwa mkazi ndi mwamuna kuti akathe kusangalala, kukwaniritsa Mau a Mulungu kuti "chulukanani ndi kuligonjetsa" dziko ndi ana amuna ndi akazi ambiri ndi moyo wamuyaya. Koma china chake chinachitika…, serpenti anabwera kwa Hava ndi kumuyesa iye, ndipo iye anagonjera ku yesero ndi kutenga za mu mtengo wa Chidziwitso opanda dalitso la Mulungu, pochita chinthu chosavomerezeka ndi serpenti; iye pokhala wantchito ndipo wofanana ndithu ndi

mtundu wa anthu. Ndipo anamunyenganso Adamu ndipo iyenso, “anadya za Mtengo wa Chidziwitso” ndi Hava, ndipo zinabweretsa imfa, osalumikizana ndi Mtengo wa Moyo. Izi zinabweretsa kugwa kwa mtundu wa anthu. Kotero, Hava anakhala ndi pakati pa mbewu ziwiri ndipo anabereka mapasa; Kaini ndi Abele. Kaini anali mwana wa mwamuna wa serpenti ndipo Abele anali mwana wa mwamuna wa Adamu.

Mtundu wa anthu utagwa, Mulungu anatemberera serpenti amene anali wamaonekedwe ofanana ndi munthu, ndipo iye anasandulika chokwawa kapena chinjoka. Mulungu anasintha lamulo la kubereka mu thupi la Hava, kotero kuti “nyengo yache ya kumwezi” ikanakhala kamodzi masiku 28 aliwonse kapena choncho; ndi kuchulukitsa ululu wake pobereka ana. Ndipo kwa Adamu, Mulungu analinso ndi chilango. Iye anatemberera wantchito wache [serpenti] kumusandulitsa iye kukhala chinthu chokwawa. Kuyambira pamenepo kupita kutsogolo, Adamu amatha kugwira ntchito ndi “kudya mkate ndi thukuta lake.” Izi zinatsiriza munda wa Edeni. [Genesis 3:8-19] Tsopano panali mbewu ziwiri pa dziko zimene zimayenera kukulira palimodzi, mpakana kukolora kotsiriza kumene Yesu anakulankhula ku Mateyu, chaputala cha khumi ndi chitatu.

Edeni anali atayika, koma kodi anataika mpakana kalekale? Mulungu anatenga Mtengo wa Moyo ndi kuika oyang’anira kusunga njira ya ku Mtengo wa Moyo, pamene Iye anachotsa Mzimu Wake mu Edeni. Dziko ladutsa mu zaka zikwi zisanu ndi ziwiri kuyambira nthawi imeneyo, koma Mulungu ndi Mulungu wobwezeretsa. Ichi ndi chimene Chivumbulutso, chaputala 21 ndi 22 chiri. Ndi Mzimu wa Mulungu kubweranso ku dziko Iye atatha kubereka banja Lake ndi kuwayesa iwo, powalora iwo kuyesedwa mu kachitidwe kamene kanali koyesa chikhulupiriro chawo kwa zaka zikwi zisanu ndi ziwiri. Koma apa tikuona Mulungu kubwera kudzakhala ndi chimene iye anabereka. Chirichonse chimene tikuchiona ngati mzinda chiri pompano. Mulungu tsopano ali ndi banja Lake kumudzi, ndiye apa akubwera ku dziko kudzakhala nawo pamodzi mu muyaya. Kachiwirinso, izi ndi zauzimu.

ZIFUNGULO ZOPANGITSA KUMVETSA MACHAPATALA AWIRI OTSIRIZA

Chaputala 21 ndi 22 cha bukhu la Chivumbulutso zikuyendera palimodzi bwinobwino, ndipo ndikovuta kuzimvetsa pokhapokha titaziyang’ana mwa njira iyi. Kuzisiyanitsa izo kukanakhala vuto lalikulu ku kuyesa kwathu wa uzimu kuti tikafike ku kufotokoza kogwirana. Chaputala 21 ndi 22 chikuyenera kuonedwa ngati chithunzi chimodzi. Kotero tisanayambe kuyesera kumvetsa machaputala awiri a Baibulo, tikuyenera kulingalira kuti kodi nzindawo ndi weniweni kapena choimirira. Izi ndi zokakamiza ngati ife tikufuna kumvetsa chimene Yohane anachiona. Mzindawo ndi wauzimu, koma kuti dziko lokhalo kapena malowo ndi enieni [kapena ogwirika].

Mzinda umene ukufotokozedwa mu machaputala awiri awa otsiriza a bukhu la Chivumbulutso ndi chimene Mulungu anachiyamba ku Genesis, bukhu loyamba la Baibulo ndipo chatsirizidwa ku machaputala awiri otsiriza a Baibulo. Kotero, ife tikuyang’ana pa mzinda ngati china chake chimene Mulungu anachita kudutsa mu nthawi, ife tikuona Mbiri ya Chiombolo Chachikulu apa. Zikubweretsa chithunzi chabwino cha ntchito zake kuyambira ku Genisis kudutsa mu nthawi, mpakana kutsiriza kwake kumapeto kwa Baibulo.

Tsopano tafika ku mathero.., mzindawo ndi mzinda wongoimirira. Chifukwa chiyani Mulungu amauonetsa kwa Yohane monga chonchi podziwa kuti ambiri sadzamvetsa? Nthawi zambiri zinthu za Mulungu zabisidwa kwa munthu wathupi, chifukwa siziri kwa iwo, koma nthawi zonse zimabweretsa chimwemwe chachikulu ndi chisangalaro kwa munthu wa uzimu pamene Mulungu aulura chinsinsi chachikulu kwa iwo, monga zalembedwera ku 1 Akorinto 2:7-14; monga tawerengera kale.

Mwa chitsanzo, chirombo chimene Yohane anaona mu machaputala osiyanasiyana a bukhu iri zinalinso zoimirira, chifukwa sakanatha kuona mzimu, kotero Mulungu anamulora iye kuona chirombo cha kuthupi, kotero kuti akamupatse chinachake mu gawo la zinthu za thupi kuti akathe kuchimasulira. Ndi njira yomweyo pa zokhudza, Yerusalemu Watsopano. Ukuoneka ngati mzinda wa thupi, kuti tikafike pa kumvetsa kwa uzimu.

Chimene chinachitika mu Edeni chinali Mulungu kuchotsa Edeni wa uzimu, koma kusiya Edeni wa thupi, “Mtengo wa Chidziwitso” pano pa dziko. Iye anachotsa Mtengo wa Moyo, chimene chinali maonekedwe auzimu amene munthu akanatha kulowamo. Inde, anali malo abwino, koma kugwa kutachitika, Iye anaika alonda kutetezera njira ya ku Mtengo wa Moyo. Kotero chimene Yohane akuchiona mu Chivumbulutso chaputala 21 ndi 22 ndi Edeni wa uzimu kubweranso ku dziko.

Ku Genesis, Mulungu anatenga mzimu wa Edeni, koma anasiya deralo. Ku Chivumbulutso, chaputala 21 ndi 22, chimene tikuchiona ndi Mulungu kubwera kudzakhala mwa ana Ake, ndi kubweretsanso Mzimu wa Edeni ku dziko. Ndi malo omwewo amene Edeni oyamba anali. Ndiloreni ndifotokozenso, **ndi zonse zauzimu.** Palibe cha thupi kapena chenicheni pa zokhudza mzinda uwu konse. Ndi onse wauzimu.

Lingaliro lotsiriza tisanafike ku mzinda uwu: Pamene Mulungu anachotsa Edeni wa uzimu, Iye sanatenge ngakhale ka nchenga kamodzi kapena chirichonse chogwirika kapena chathupi. Pamene mzinda uwu ubwera kutsika kuchokera kumwamba, palibe chimodzi chogwirika kapena chathupi chimene chidzatsika. Ndi Mulungu kubweranso ku dziko, ndi mzindawo ndi chimene iye wabereka kudutsa mu nthawi ndipo watsirizika apa.

Tsopano tiyeni tifike ku Chivumbulutso, chaputala 21 ndi 22 kuchokera pa maimidwe awa, ndi kuziona izo zikusandulika zowala ngati krustalo..., ngati galasi. Ambuye atthandize ife.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHA MAKUMI AWIRI NDI CHIMODZI

Dziko ndi ntchito ya manja a Mulungu. Iye anaigwiritsa ntchito mu m’bado wa mbiriisanayambe kuyesera matupi angelo. Pa nthawi imeneyo satana, mngelo wamphamvu, ndipo gawo limodzi la magawo atatu la angelo analephera kusunga Mau a Mulungu ndi kubweretsa chiononge ko chachikulu pa dziko lonse lapansi. Zinali mu nthawi imeneyo pamene nyama zambiri zimangoyenda pa dziko. Mu malo osungaramo zinthu za kale pa dziko, ife tikuona mafupa ochuluka a zinyama zimene zinakhala pa dziko m’bado wa mbiriisanakhale. Satana ndi angelo ake anagwa, ndikubweretsa chiweruzo cha Mulungu pa m’bado umenewo, ndipo zonse [zathupi] zolengedwa zamoyo zinafa, ndipo Mulungu anaponya dziko lapansi kutali

ndi dzuwa, ndipo m'dima unali pa dziko, ndipo dziko linasungunuka pamene limazungulira mulengalenga kwa mwinamwake mamilioni a zaka mu m'dima.

Ku Genesis woyamba, ife tikuona Mulungu akuyamaba kubweretsa dziko m'malo mwake. Mulungu akuyamba munda umene anautcha munda wa Edeni. Unali wokongola wosafokozeka, ndi pamene nthawi inayamba monga tikuidziwa iyo. Izi zinali kale chigumula chisanachike chimene chinasintha dziko ku chimene tiri nacho lero.

Chigumula chisanachitike, dziko limathiriridwa ndi chinyezi, kapena mame; pamene dzuwa limalowa, mpweya umaziziritsa, ndipo zimapangitsa mame pa dziko. Ndi m'mene Mulungu amathirira dziko. Panalibe **mvula nthawi ya chigumula isanafike** [Genesis 2:6-7], koma panali chifunga chimene chimayenda kuchokera ku dziko kupita kuthirira nthaka yonse.

Chigumula chisanayambe ndipo mu Munda wa Edeni pamene Mulungu anaika munthu pa dziko, dongosolo Lake linali loti dziko lonse lidzaze, ndi kukhala malo amene nyengo ndi chirichonse zikhale zabwino, koma mpando wache waufumu ukhale pa dziko, koma tchimo linabwera ndipo dongosolo lache linaimitsidwa.

Tsopano tiyeni tiyang'ane pa mfundo ina mu Bukhu la Chivumbulutso yokhudza nthawi…, miyezi 42, zaka zitatu ndi theka, kapena masiku 1260, zonse zikukwana masiku 360 pa chaka. Kalendala weniweni wa Mulungu ndi masiku 30 pa mwezi. Khumi ndi chiwiri kuchulukitsa ndi 30 zikukwana 360, chimenecho chinali chiwerengero cha masiku pa chaka. Ife tikudziwa kuti madigiri 360 amapanga chozungulira chonse. Ndi m'mene Mulungu anayambira chinthu ichi. Masiku makumi atatu pa mwezi, masiku 360 pa chaka, ndi zolondora, koma tsopano tiri ndi masiku 365 ¼ zimene zikuonetsera kuti dziko lazunguzidwa kuchoka ku chiyanjano chake choyamba ndi dzuwa; chimene chikuonetsera kuti liri kunja kwa kupitiriza ndipo lachoka, koma Yohane analiwonanso langwiro mu masomphenya.

Ku Genisis 1:6-8, Mulungu anagawa madzi ndi kuwaika pamwamba ndi pansi pa thambo [kumwamba pamene maso athu amaona, pamatchedwa pansi pathambo]. Apa pamayeretsa kutentha kwa dzuwa ndi kupanga nyengo ya bwino. Kotero mbewu imene ina anasungunuka kwa mibado inayamba kutuluka, kupanga Munda wa Edeni, malo angwiro, koma ochepa. Kotero Mulungu adalenga mamuna ndi mkazi ndi kuwaika iwo m'munda uwu, ndi kuwauza iwo kuti achuluke ndi kuligonjetsa [kuchulukana] dziko [kutanthauza kuti inali itadzaza nthawi iyi isanafike; inali nthawi ya m'bado wa mbiriisanayambe], **NDI KULICHOTSA ILO**. Mwa kulankhula kwina, pamene iwo amachulukana ndikumafuna malo lochuluka, kugonjetsa dziko ndi kupanga Munda wa Edeni PALIPONSE pa dziko, koma munthu anachimwa ndi kutaya ulamuliro wache pa dziko komabe dziko sirinachotsedwe. Koma mu masomphenya a Yohane, anaona dziko likuchotsedwa ndipo unali Munda wa Edeni pa dziko lonse. Nkhaniyi ndi yopsinjika apa, koma ikhala ngati yowala ngati Krusatalo pamene tikhala tikuphunzira palimodzi.

Ngati inu mutawerenga chaputala choyamba cha Genesis ndi kutenga tanthauzo lenileni la icho, inu mudzaona m'mene Mulungu anasiyanitsira madzi amene anali pa dziko, makamaka mu Munda wa Edeni, kulitenga, ndikupangitsa Madera owuma kuwonekera, ndi zina zotero. Dongosolo lapachiyambi la Mulungu ndi la pa dziko kuti pakhale pangwiro ndi nyengo yangwiro, koma munthu anachimwa motsutsana ndi Mulungu ndipo Iye anabweretsa chiweruzo chake ndi chigumula. Ife tikadali ndi muyeso omwewo wa madzi umene Mulungu analenga zaka mamilioni apitawo. Madzi ndi chinthu chimene inu simungathe kuononga. Inu mukhoza

kuumitsa ndikuwapanga kukhala cholimba. Inu mukhoza kuchiwiritsa icho, ndipo chidzapita kukhala chifunga. Inu mukhoza kuchitsanulira pa dziko ndipo icho chidzalowa mu nthaka; koma mpweya umangochitenganso ndipo potsiriza chidzapezanso njira yake kupita ku nyanja. Kenako chikubweranso mu njira ya mvula, chifunga, ndi zina zotero.

Lero tiri ndi mwachidule magawo awiri mwa magawo atatu a dziko odzaza ndi madzi. Yohane anaziona izo mu maonekedwe ake a pachiyambi, ndi dziko lomwelo, malo omwewo, koma palibeponso nyanja.

Vesi 1: *"Ndipo ndinaona m'mwamba mwatsopano ndi dziko latsopano; pakuti mwamba moyamba ndi dziko loyamba zidachoka, ndipo kulibenso nyanja."*

Ife tiri ndi madzi ambiri pa dziko iri nthawi ino okwana dziko lonse. Ife sitikudziwa ngakhale kuya kwa nyanja malo osiyanasiyana. Madzi ali pano pa dziko tsopano. Yohane anaona dziko iri ndipo panalibe nyanja. Chinachitika ndi chiyani? Funso labwino sichoncho? Tsopano tiyeni tiyankhe funsoli. Kodi madzi onsewa anachokera kuti? Yankho ikupezeka ku Genesis, chaputala 6 ndi 7, pamene tikuwerenga zochitika za mu chigumira chachikulu. Mu chaputala cha chisanu ndi chiwiri, vesi la khumi ndi chimodzi, tikuwerenga zimene zinachitika. Akuti "Akasupe onse a pansi anaonongeka ndipo mazenera a kumwamba anatseguka." Izi zikutanthauza kuti madzi onse amene anakhala ngati lamba wa mpweya anagwa ku dziko kwa masiku makumi anai usana ndi usiku, kulenga chigumula, ndi chifukwa chake tiri ndi nyanja zikuluzikulu lero. Dziko linaponyedwa kuchoka m'malo ake ndipo chigumula chinafika, kusintha nyengo kuchokera pokhala ya ngwiro mu Munda wa Edeni kufika ku chimene tiri nacho lero. Kotero tiri ndi nyanja lero, chifukwa madzi amene anali mu mulengalenga anagwa ku dziko, koma apa pa Chivumbulutso makumi awiri ndi chimodzi, tikuona kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano ndipo palibenso nyanja. Zabwezeretsedwanso pa chiyambi.

Pamene kumwamba kwatsopano uku ndi dziko zitsika ndipo tikupita ku umuyaya wa Mulungu, Iye akuika dziko lakale iri m'malo mwake. Iye akuyibwezeretsa mu njira kufupi ndi dzuwa kumene linapanga kuzungulira kamodzi dzuwa masiku 360 aliwonse m'malo mwa masiku 365 ¼ . Mulungu sadzaononga madzi amene ali pa dziko. Iye adzawatenga ndi kupanga chilamba cha mpweya chimene pakati pa ife ndi dzuwa. Iye adzachotsa madzi onse, monga Iye anachitira mu Edeni, kuyeretsa kutentha kwa dzuwa ndikupangitsa nyengo kukhala imodzimodzi pa dziko lonse. Sipadzakhalanso malo pa dziko pamene padzakhala madzi ogwirana. Sipadzakhalanso pa dziko chipululu, chifukwa Mau akuti zipululu zidzaphuka ngati duwa. Mulungu adzapanga nyengo yabwino kwa anthu athupi kuti akhalemo, ndipo zimenezo zidzakhala pa dziko. Apa ndi pamene madzi ochokera ku nyanja amapita. Sipadzakhalanso nyanja, koma padzakhala madzi ambiri; chifukwa mu Munda wa Edeni munali mitsinje ya madzi. Padzakhala mitsinje. Zidzakhala ngati paradaizo pano pa dziko. Ndi chimene Yohane anaona mu gawo la dziko lapansi.

Vesi 2: *"Ndipo ndinaona mzinda woyerawo, Yerusalemu watsopano, ulikutsika Kumwamba kwa Mulungu, wokonzeka ngati mkwatibwi wokometsedwera mwamuna wache."*

Pamene Yohane anaona mzinda, Yerusalemu watsopano, ukutsika, unakonzedwa ngati Mkwatibwi okonzedwera mwamuna wache. Koma oyeramtima a Mulungu ali kale pa dziko. Anthu amene anabadwa ndi kukhala mu mileniamu adakali pa dziko.

Uyu ndi Mulungu, Mzimu wa Muyaya, Yehova, Wamuyayayo, zimenezo zakhala ziri choncho ndipo zidzakhala choncho, kutsika pa dziko ndi kudzakhala pamodzi ndi amene

awaombola. Kupezeka kwache kumangobweretsa kutsiriza ndi kuonetsera chimene Iye wakhala ali kuchita kuyambira ku chiyambi cha nthawi. Ngakhale Yohane anaona mzinda uwu ukutsika, ife tikudziwa kuti unali kale pano. Kotero kumasulira kwa vesi lachiwiri ndi uku: Kudzoza kwa Mulungu kubwera pa oyeramtima pamene Iye akusuntha mpando Wake ku dziko. Izi zikuwalira dera la mamailosi masikweya1500. Oyeramtima a ulemelero amakhala apa, monga mudzamvetsera kuchokera ku kuwerenga chaputala cha 21 ndi 22. [Kumbukirani apa, chirombo chimene Yohane anachiona mu machaputala ena a bukhu iri sichinali chenicheni, koma chongoimirira, choncho ndi m'mene ziriri ndi mzinda. Ndi Mzimu wa Mulungu kubwera pa chimene chiripo kale apa.]

Kumayambiriro kwa ulamuliro wa mileniamu Yesu akubwera ku dziko, koma Mulungu, Mzimu wa Muyaya, udakali mu gawo la mwambamwamba. Koma apa, ulamuliro wa mileniamu ukatha, Mulungu mwiniwache, Mzimu wa Muyaya, akubwera ku dziko; osati munthu Khristu Yesu, koma Mulungu. Yohane anaona Mulungu akubwera ku dziko ndikutenga malo ake. Ndi Ufumu umenewo wa Mulungu umene Mulungu amabweretsa ku dziko. Inu munabwera muchimenecho pamene inu munakhala mu chiyanjano ndi Mulungu. Inde, ndi Mulungu kusuntha likulu Lake kupititsa ku dziko pamene m'bado wa Muyaya ukuyamba.

Ahebri 11:8-10 akuti, *"Ndi chikhulupiriro Abrahamu, poitanidwa, anamvera kutuluka kunka ku malo amene adzalandira ngati cholowa; ndipo anatuluka kunka ku malo amene adzalandira ngati cholowa; ndipo anatuluka wosadziwa kumene amukako. Ndi chikhululupiriro anakhala mlendo ku dziko la lonjezano, losati lache, nakhalira mahema pamodzi ndi Isake ndi Yakobo, olowa nyumba pamodzi ndi iye a lonjezano lomwelo; pakuti analindira mzinda wokhala nao maziko, m'misiri wache ndi womanga wache ndiye Mulungu."*

Abraham anali ndi vumbulutso la mzinda uwu. Malo amene iye anapita kukauyang'ana, mu dziko la Kanani, ndi malo omwewo amene mzinda wa Mulungu udzakhala mu nthawi imeneyo. Kungoti siinali nthawi yake mu tsiku la Abraham.

Vesi 3: *"Ndipo ndinamva mau akuru ochokera kumpando wa chifumu, ndi kunena Taonani chihema cha Mulungu chiri mwa anthu; ndipo adzakhalitsa nawo, ndi iwo adzakahala anthu ache, ndi Mulungu yekha adzakhala nawo, ndi Mulungu wawo."* Vesi 2 ndi 3 zikuyendera pamodzi. Ndi Yerusalemu uyu Watsopano kutsika, Mulungu kubwera kudzakhala pa dziko. Mau a Mulungu akuyenera kupitirira. Sanganene chinthu china pena ndi kulankhula china pena. Zikuyenera kusunga kupitirira kwa lingaliro. Ife tachita ndi dziko latsopano. Tsopano tidzachita ndi Yerusalemu Watsopano kutsika ndipo Mulungu kuyamba kukhala pa dziko.

Tiyeni tiwerenge lemba lina ku Ahebri limene likugwirizana ndi Yerusalemu Watsopano. Ife tikuonetserani inu kuti uwu si mzinda wa thupi umene Yohane anauona ukutsika; koma chirichonse chimene chitsika, chimatsikira ku dziko la thupi.

Taonani ichi, chifukwa Mau a Mulungu akuyenera kukhala mu mzere umodzi. Yerusalemu Watsopano sangakhale chinthu mu malo amodzi ndi chinthu china mu malo ena. Zikuyenera kukhala chinthu chomwecho kudutsa mu njira yonse. Ahebri 12:22- *"Komatu mwayandikira ku phiri la Zioni, ndi Mzinda wa Mulungu wamoyo, Yerusalemu wa Kumwamba, ndi kwa unyinji wochuluka wa angelo."*

Ine ndikufuna ndikufunseni inu funso. Pamene mukhala mu chiyanjano ndi Mulungu, kodi munapitako ku Yerusalemu, ku Phiri la Zioni? Ayi, Inu simunapite kwina kulikonse; koma

munapita kwinakwake mu Mzimu. Akuti inu mwafika kumene kuli angelo osawerengeka. Ine sindinaonepo m'modzi, kodi inu munamuona? Akuti inu mwafika ku mzinda wa Mulungu wa Moyo. Pamene muvomereza Yesu Khristu, inu mumabwera mu mzinda umenewo wa Mulungu wa Moyo. Kodi mudaona chiyani pamene munabwera mu icho? Inu simudaone chirichonse. Koma munabwera mu mzinda wa Mulungu wa Moyo. Inu munasandulika gawo la izo. Koma chinthu chimene ine ndikufuna kuti muone ndi ichi…, kuti inu munafika ku icho ndipo simunachione icho.

Khalani olingalira tsopano, kodi bwanji Yohane akananyamulidwa ndikutengedwa mu Mzimu ku phiri lalitali ndipo mngelo ndikuti, "Ine ndikufuna ndikuonetsere mzinda wakumwamba, Yerusalemu Watsopano." Ngati Mulungu sanamupatsire Yohane masomphenya a chinachake chogwirika mu masomphenya ake; kotero Yohane akanati, "Ine sindinaone chinthu." Ife tikanakhala tikuwerenga lero pamene Yohane anatengedwa mu Mzimu kukaona Yerusalemu Watsopano, ndipo iye sanaone chinthu. Tsopano tikanakatenga bwanji lingiriro la Mulungu ndi ganizo la Mulungu za chimene Yerusalemu Watsopano ali? Koma Mulungu anamulora iye kuona masomphenya a chinachake ngati kuti chinali chogwirika, kuti tikathe kuchimasulira kwa inu, koma chinali chonse chogwirika.

Ahebri 12:23-24- *"Ndi kwa msonkhano wa onse ndi Mpingo wa obadwa oyamba olembedwa m'Mwamba, ndi kwa Mulungu woweruza wa onse, ndi kwa mizimu ya olungama oyesedwa angwiro, ndi kwa Yesu, Nkhoswe ya Chipangano Chatsopano, ndi kwa mwazi wa kuwaza wakulankhula chokoma choposa mwazi wa Abele."*

Ife sitingathe kusintha Mau a Mulungu. Mau a Mulungu akuyenera kukhala woona, ndipo akuyenera kupitirira. Inu munabwera ku Yerusalemu Watsopano, mu mzinda; kenako munabwera ku msonkhano waukulu; kenako munabwera ku mpingo wa obadwa oyamba umene uli kumwamba. Kenako inu munabwera kwa Mulungu amene ali Oweruza wa onse ndi kwa mizimu ya anthu olungama okhala angwiro, kenako kwa Yesu, mkhala pakati wa pangano latsopano. Inu munabwera ku zonse izo pamene munabwera kwa Mulungu, pamene munasiyana nazo za dziko ndikunena kuti, "Ine ndidzavomereza Yesu ndi Mau ake," kenako inu munabwera mu mzinda Yerusalemu Watsopano. Kodi mwaonapo chirichonse? Ayi, koma kwa Yohane mu masomphenya ake, zinali zogwirika. Unali mzinda wathupi.

Ine ndikufuna ndikuonetsereni inu zina zimene Yohane anaziona pamene Mzinda umenewo unatsika. Unali wowala ngati galasi. Pamene mzinda watsopano unabwera mu vesi 2 ndi 3, chinali chiyani chimene chinatsika? Anali Mulungu Wankulu amene anabwera ku dziko kudzakhala pakati pa anthu ake, kudzaonetsera mphamvu zache za oyeramtima Ake kudutsa mu mibado. Tsopano ife tiona "mzinda" uwu ukukhala wowala ngati krustalo. Alemekezeke Ambuye!

Vesi 4: *"Ndipo adzawapukutira misozi yonse kuichotsa pamaso pawo; ndipo sipadzakhalanso imfa; ndipo sipadzakhalanso maliro, kapena kulira, kapena chowawitsa; zoyambazo zapita."*

Imfa yathetsedwa. Kotero sikudzakhalanso imfa pakati apa mafuko athupi. Iwo sadzafanso. Chifukwa chiyani? Mulungu mwini wa moyo, wabwera ku dziko.

Kodi dziko linapita? Ayi, zinthu zokhazo zakale zinapita, koma chidziko chidakali pompano. Zonse za izi kudutsa mu vesi 8 zikuyendera limodzi.

Vesi 5: *"Ndipo Iye wakukhala pa mpando wachifumu anati, Taonani, ndichita zonse zikhale zatsopano. Ndipo ananena, Talemba; pakuti Mau awa ali okhulupirika ndi woona."*

Vesi 6: *"Ndipo anati kwa ine, Zatha. Ine ndine Alefa ndi Omega, woyamba ndi wotsiriza. Kwa iye wakumva ludzu ndidzampatsa kuti amwe ku kasupe wa madzi a moyo kwa ulere."*

Vesi 7: *"Iye wakulakika adzalandira izi; ndipo ndidzakhala Mulungu wache, ndi iye adzakhala mwana wanga."*

"Iye adzakhala mwana wanga," sizikutanthauza kuti ana ake akazi sadzakhala kumeneko. Inu mukhoza kunena "Iye amene agonjetsa adzakhala ndi zonse ndi kukhala mwana wa Mulungu," chifukwa zikukhudza *ana akazi* ndi amuna, mu kulankhula kwina, "Ana a Mulungu."

Vesi 8: *"Koma amantha ndi osakhulupirira, ndi onyansa, ndi ambanda, ndi achigololo, ndi olambira mafano, ndi onse amabodza, cholandira chawo chidzakhala m'nyanja yotentha ndi moto ndi sulfure; ndiyo imfa yachiwiri."* [Mavesi 11-15 a chaputala 20 ndi ofanana ndi vesi la 8 apa, ndipo afotokozedwa mu chaputala 20.]

Vesi 9: *"Ndipo anadza m'modzi wa angelo asanu ndi awiri akukhala nazo mbale zisanu ndi ziwiri, zodzala ndi miriri yotsiriza isanu ndi iwiri; ndipo analankhula ndi ine, nanena Idza kuno, ndidzakuonetsa mkwatibwi, mkazi wa Mwanawankhosa."*

Kachiwirinso *"m'modzi mwa asanu ndi awiri"* si m'modzi mwa m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri athupi, koma ndi m'modzi mwa anegelo asanu ndi awiri auzimu." Nthawi iyi Yohane sadzaona Mulungu akubwera ku dziko, koma iye ayamba kuona chinachake chogwirika chikuoneka. **Sikuti pali ma Yerusalemu awiri.** Pali m'modzi ekha, koma inu simungathe kuona Yerusalemu wa Uzimu wa Mulungu. Pamene mngelo anati, *"Idza kuno, ndidzakuonetsa mkwatibwi, wa Mwanawankhosa,"* Yohane kwenikweni anayamba kuona chinachake mu masomphenya chimene akanatha kuchilemba, kuti tikathe kutenga tanthauzo la icho. Chimene icho chiri ndi Mulungu kubwera kutsika mu maonekedwe ena ake ndipo oyeramtima onse ali pomwepo ndi Iye, chimene chimapanga mzinda umenewo.

Vesi 10: *"Ndipo ananditenga mu Mzimu kunka ku phiri lalitali, nandiwonetsa mzinda wopatulikawo, Yerusalemu wotsika m'Mwamba kuchokera kwa Mulungu."*

Vesi 11: *"Ndipo unakhala nawo ulemerero wa Mulungu; kuunika kwache kunafanana ndi mwala wa mtengo wache woposa, ngati mwala wayaspi, wonyezimira, ngati khrustalo."*

Ngati chinachake chiri chonyezimira ngati krustalo, njira yokhayo tingathe kuchiona ndi, ndi kuti chimabweza kuwala kuchokera kwa icho. Inu mutenge galasi lowala ndi kuyang'ana kupyolera mwa iyo, simunathe kudziwa kuti iri pamenepo pokhapokha kuwala kutawalira kwa ilo, chifukwa ndi lonyezimira ngati krustalo. Mzinda uwu umene Yohane adawuona udali wonyezimira ngati krusatalo. Kodi inu mudapita kuti pamene munakhala moona ndi Ambuye? Inu mudabwera mu mzinda uwu, koma simunathe kuuona, chifukwa kudzoza kwa Mulungu sikunaikidwe pa iwo. Mulungu sanabwere ndi kudzakhala ndi munthu. Ndi chonse chimene Mulungu wachiombola. Iye anatsika ndi kukhala ndi woomboledwa ake mu m'bado uno wamuyaya. Mngelo asanamuonetsere Yohane mzinda wa mkati, umene ndi Mkwatibwi, iye anamuonetsa iye mzinda wakunja.

Vesi 12: *"Nukhala nalo linga lalikuru ndi lalitali, nukhala nazo zipata khumi ndi ziwiri, ndi pazipata angelo khumi ndi awiri, ndi maina olembedwapo, ndiwo amina a mafuko khumi ndi awiri a ana a Israeli."*

Tisanapitirire ndi uthenga uwu tikuyenera kupanga lingaliro kuti "Kodi ndi mzinda weniweni?" Kodi ndi chinachake chimene ife tikhoza kuchiona? Vesi iri likuti unali nalo linga

lalikulu ndi lalitali. Kodi padzakhala khoma lalikulu limene tikhoza kuyendapo ndi kutsamira? Kodi zidzakhala choncho, kapena udzakhala mzinda; ufumu wa Mulungu, umene tinalowamo pamene tinayamba kuyenda molondora ndi Mulungu. Ndi chimene chiri. Ndi ufumu wauzimu wa Mulungu umene ife tinalowamo. Palibe mzinda weniweni umene ukutsika, chifukwa maziko a linga atchulidwa kuchokera kumaina a atumwi a Mwanawankhosa. Pamene Petro anachoka, kodi Iye ananyamula thumba la simenti, ndi miyala kuti akaike maziko? Ayi. **Koma iye ananyamula chikhulupiriro mu mtima mwache chimene chinayesedwa kudzera mu mayesero woopsa. Iye ananyamula vumbulutso.** Iye ananyamula mwala inde, vumbulutso la Mau. Ndikufuna ndikuonetsereni m'mene Mulungu anazifanizira izi. Pali zipata zitatu pa mbali iriyonse ya mzinda mkati mwa khoma.

Mu Bukhu la Numeri, chaputala chachiwiri, Mose anawauza ana a Israeli m'mene angakhalire mzigono. Iwo amayenera kukhala mozungulira chihema mu chipululu. Kodi ana a Israeli amachita chiyani kukhala mozungulira chihema? Anali alonda a Mulungu. Msirikali aliyense mu Israeli amayenera kufa chirichonse chisanalowe mu chihema. Chihema chinali mkati mwa chigono. Numeri 2:1-2- *"Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni, nati, Ana a Israeli azimanga mahema awo yense ku mbendera yache, ya chizindikiro cha nyumba ya kholo lache, amange mahema awo popenyana ndi chihema chokomanako pozungulira."* Panali zizindikiro zinai. Chizindikiro cha pfuko la Yuda chinali mkango. Chizindikiro china chinali ng'ombe. Ife taphunzira izi ku chaputala chachinai cha bukhu iri. China chinali nayo nkhope ngati ya munthu ndipo china chinali ngati chiombankhanga chouluka. Mulungu anaonetsera dongosolo la m'momwe iwo angakhalire. Paulo akutiuza ife chimene Mulungu anamuuza Mose mu Bukhu la Ahebri. Iye anati *"Panga chirichonse mwa maonekedwe amene unawaona kumwamba."* Chimene Mose anachiona kumwamba chinali chithunzi cha Mpingo, woomboledwa a Mulungu. Tiyeni tiwerengenso ku Numeri. Numeri 2:3-*"Ndipo iwo akumanga mahema awo ku m'mawa kotuluka dzuwa ndiwo a mbendera a chigono cha Yuda, monga mwa makamu awo."* Ndim'mene iwo amene anali pansi pa chizindikiro chimenecho amakhalira. Panali mafuko atatu kapena zipata zitatu ku mbali iriyonse. Zinayi zitatu zimapanga khumi ndi ziwiri. Panali mbali zinai ku khoma. Mafuko anai amakhala pansi pa chikwangwani. Mkati mwa chigono munali chihema chimene chinamangidwa mu chipululu. Kumbukirani kuti ku Chivumbulutso, kuti chihema cha Mulungu chatsika pakati pa anthu.

Tiyeni tiwerenge Numeri 2:10. *"Mbendera ya chigono cha Rubeni ikhale kumwera monga mwa makamu awo."* Zimenezo ndi mbali ziwiri kulonderedwa.

Numeri 2:18 akuti, *"Mbendera ya chigono ya Eferemu* izikhala *ku madzulo monga mwa makamu awo."* Kumeneko ndi kum'mawa, kumwera ndi kumadzulo, chimene chikutanthauza kuti mbali zitatu zikulonderedwa.

Numeri 2:25 akuti, *"Mbendera ya chigono cha Dani izikhala kumpoto monga mwa makamu awo."* Kumeneko ndi ku m'mawa, kumwera, kumadzulo ndi kumpoto- mbali zonse zinai kulonderedwa. Pali mafuko khumi ndi awiri a ana a Israeli. **Chimene anachita kunali kupanga linga limene palibe aliyense amene akanatha kudutsa ndi kulowa mu chihema chimenecho.** Anali ndi mafuko atatu mbali iriyonse. Ngati inu mutafuna kuwerenga izi, inu mudzapeza zambiri za izo mu Numeri Chaputala chachiwiri.

Ine ndikufuna ndikuonetsereni chimene Yohane anaona mu Bukhu la Chivumbulutso. Yohane, pokhala muyuda, anadziwa zambiri za izi kusiyana ndi m'mene ife tingadziwire. Chifukwa

chimene ine ndikudutsira mu izi ndi kuti ife Amitundu tikhale odziwa izi za m'mene Israeli anakhalira mu chigono ndi m'mene chihema chinaliri, ndipo mudzaona chimene Mulungu anamuonetsera Yohane chimene chinatsika mu chaputala cha makumi awiri ndi chimodzi cha Chivumbulutso. Kodi inu mukutha kuona m'mene akhalira? Mafuko atatu mbali iriyonse. Kachiwirinso Chivumbulutso 21:12 akuti, *"Nukhala nalo linga lalikuru ndi lalitali, nukhala nazo zipata khumi ndi ziwiri, ndi pazipata angelo khumi ndi awiri, ndi maina olembedwapo, ndiwo amina a mafuko khumi ndi awiri a ana a Israeli."* Taonani m'mene anakhalira apa ku Chivumbulutso. Ndi chimodzimodzi m'mene anakhalira mu thupi.

Vesi 13: *"Kum'mawa zipata zitatu, ndi kumpoto zipata zitatu, ndi kumwera zipata zitatu, ndi kumadzulo zipata zitatu."*

Monga m'mene zinaliri pamene Mose anawauza m'mene iwo angakhalire; panali zipata zitatu pa mbali iriyonse, kupanga mafuko khumi ndi awiri a ana a Israeli. Kodi zikuonetsera chiyani? Dongosolo iri la chipulumutso linayamba ndi pfuko la Israeli. Sikuti panalibe anthu amene sanapulumutsidwe pfuko la Israeli lisanafike. Iwo amene anafa chigumula chisanafike amene maina awo analembedwa mu bukhu la moyo anaukitsidwa mu chiukitsiro choyamba ndikukhala gawo la woomboledwa a Mulungu. [Mateyu 27:51-53]

Tsopano tiyeni tione olemba Uthenga amene analemba zimene Yesu ananena ndi kuchita, Bukhu la Machitidwe lisanakhale. Kodi tirinawo angati olemba Uthenga? Mateyu ndi mkango. Marko ndi ng'ombe. Luka ndi munthu, wochiritsa; ndipo Yohane amaimirira chiombankhanga chouluka. Awa ndi alonda anai kulondera Bukhu la Machitidwe, Ufumu wa Uzimu wa Mulungu umene Mpingo woyamba unabweramo mu masiku oyambirira; m'modzi pa mbali iriyonse ya Mpingo pa dziko. Bukhu la Machitidwe likutionetsera kuti Mpingo umenewo ukuchita.

Mu chaputala cha chinai cha Chivumbulutso ife tikuona zinyama zinai zolondera. Iwo akulonderabe chinachake mu nthawi ino. Mkango, ng'ombe, munthu, chiombankhanga chouluka akukhala mozungulira ndi kulondera chihema chenicheni kapena kachisi wa Mulungu. Iwo adakali onse mu dziko mutsiku lotsiriza. **Otsiriza wabwera mu tsiku lathu pansi pa uthenga wa wanthenga wa chisanu ndi chiwiri, William Branham. Chiombankhanga chouluka chimenecho chinabwera kudzalondera choonadi cha Baibulo.**

Kodi mukutha kuona zipata? Ndi mafuko khumi ndi awiri a Israeli kuyamba dongosolo la uzimu la Mulungu. Pamene anthu amanga mzinda mu nthawim yakale, iwo amayamba aika zipata. Kenako iwo amamanga linga mozungulira zipata, kuti khoma lirimbitse zipata.

Ine ndikufuna ndikuonetsereni dongosolo la Mulungu pamene akumanga mzinda uwu ku Chivumbulutso 21. Zinali mu chinyumbacho kudutsa mu njira yonse. Yohane anachiona icho mu maonekedwe ake angwiro. Kodi zipata zinaikidwa liti? Izo zinaikidwa ku Chipangano Chakale? Anali Mulungu kuchita ndi mitundu khumi ndi iwiri ya Israeli.

Kodi mukuona kuti zipata zinali ana a Israeli pamene iwo anaima ndi Mau a Mulungu ku Chipangano Chakale? Funso linafunsidwa ku Aroma, "Kodi chipindulanji kukhala mu Yuda?" Paulo akuti, "Zambiri monse monse: choyamba kuti mau a Mulungu anaperekedwa kwa iwo." [Aroma 3:2] Chinali chiyani? Vumbulutso loona la Mulungu m'modzi linaperekedwa kwa Israeli. Iwo anakhala woona ku vumbulutso limenelo la Mulungu m'modzi, ndipo adakali kuima ndi chimenecho lero. **Kotero mwa Mulungu, mkati mwa ufumu wa Mulungu, zimenezo zikuika zipata za mzinda umenewo.**

Vesi 14: *"Ndipo linga la mzinda linakhala nawo maziko khumi ndi awiri, ndi pomwepo maina khumi ndi awiri a atumwi khumi ndi awiri a Mwanawankhosa."*

Khoma la mzinda linali ndi maziko khumi ndi awiri. Zipata zinaikidwa mu nthawi ya Chipangano Chakale. Maziko a khoma anaikidwa mwa kulalikira, mwa moyo, ndi uthenga wa atumwi khumi ndi awiri pamene amamvetsera Petro pa tsiku la Pentekosite. Pamene Petro anaimirira, iwo anati, "Tidzachita chiyani, amuna inu abale, kuti tipulumutsidwe?" Kodi Petro anaimirira ndi ndani? Ndi khumi ndi m'modzi. Pamene Petro anaima ndi mkhumi ndi m'modziwo anati, *"Lapani, batizidwani yense wa inu mu dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera."* [Machitidwe 2:38] Ndipo tsiku limenelo miyoyo zikwi zitatu inabwera, koma anali onse a Yuda, kupatula otembenuka, amene anali Amitundu kutembenukira ku Chiyuda.

Apa panabwera atumwi kulalikira zaka zoyambira pentekosite atatha. Iwo amachita chiyani? Zipata zinali zitaikidwa kale. Pomanga mzinda inu mumaika zipata, ndipo khoma limagwira malinga amenewo motetezera. **Vumbulutso limene linalalikidwa ndi atumwi khumi ndi awiri a Mwanawankhosa ndi maziko a khoma ndipo adzagwira zipata motetezera.** Ichi ndi vumbulutso la Mulungu m'modzi, ndi chonse chimene Mulungu anachiyamba kuyambira ku Chipangano Chakale.

Pangano limene Mulungu anapanga –kodi linapangidwira ndani? Kwa Ayuda. Mulungu sanayambepo apanga pangano ndi Amitundu. Ife timangopulumutsidwa chifukwa cholumikizitsidwa mu pangano Lake ndi Abrahamu. Ife Amitundu timabwera ku vumbulutso la Mulungu kupyolera ku chimene chinaperekedwa ku akuru khumi ndi awiri. Vumbulutso loyamba limene limasoweka kubwera mu ufumu wa Mulungu linali loti **Mulungu ndi Mulungu m'modzi.** Mulungu anati, *"Mvera iwe, O Israeli, Ambuye Mulungu wako ndi Mulungu m'modzi."* Maziko anaikidwa pa khoma pa vumbulutso lakuti Mulungu ndi Mulungu m'modzi monga atumwi analalikira. Uthenga woona unayamba ndi zomwe Mulungu anachita ku Chipangano Chakale, ndi kuzibweretsa mwatsopano ku Chipangano Chatsopano.

Kodi muona chimene zipata za mzinda umenewo chiri? Ndi miyoyo, ndi zina zotero za akuru khumi ndi awiri a Israeli. Kodi maziko ndi chiyani? Ndi uthenga ndi ulaliki umene unalalikidwa ndi atumwi achiyuda a Mwanawankhosa.

Vesi 15: *"Ndipo iye wakulankhala ndi ine anali nao muyeso, bango lagolidi, kuti akayese mzindawo, ndi zipata zache, ndi linga lache."*

Vesi 16: *"Ndipo mzinda ukhala wampwamphwa; utali wake ulingana ndi kupingasa kwake: ndipo anayesa mzinda ndi bangolo, mastadiya zikwi khumi ndi ziwiri; utali wake, ndi kupingasa kwake, ndi kutalika kwake ziringana."*

Vesi 17: *"Ndipo anayesa linga lake, mikono zana mphambu makumi anai kudza zinai, muyeso wa munthu, ndiye mngelo."*

Kodi muyezo umenewo ukuonetsera chiyani? Ukuonetsera muyeso weniweni wa malo amene Mulungu adzaika likulu lake pamene Iye abwera ku dziko. Izi ndi ku thupi, koma ku uzimu zikuonetsera muyezo winawake, kudziwidwiratu ndi Mulungu, kuti pali nambala inayake yoti ibwere kudzapanga mzinda wathunthu wa Mulungu, onse amene maina awo ali mu bukhu la moyo. Mulungu anati Iye akuwadziwa amene ali Ake. Kukula kwa mzinda kukuonetsera kudziwiratu kwa Mulungu. Pali chiwerengero chinachake cha miyoyo chimene chikuyenera kulowamo.

Mastadiya zikwi khumi ndi ziwiri ndi pafupifupi ma mailosi masikweya1500, mzinda wa mamailosi masikweya 1500. Malo amene likulu la Mulungu lidzakhale ndi Kum'mawa Chapakati, penipeni pamene panali Munda wa Edeni pachiyambi. Ma mailosi 1500 ndi kuyeza kwenikweni. Kudziwiratu ndi kuyeza kwa uzimu.

Vesi 18: *"Ndipo mirimo ya linga lake ndi yaspi; ndi mzindawo ngwa golidi woyengeka, wofanana ndi mandala oyera."*

Vesi 19: *"Maziko a linga la mzinda anakometsedwa ndi miyala ya mtengo, ya mitundu mitundu; maziko oyamba, ndi yaspi; achiwiri, ndi safiro; achitatu, ndi kalikedo; achinayi, ndi smaragido."*

Vesi 20: *"Achisanu, ndi sardonu; achisanu ndi chimodzi, ndi sardiyo; achisanu ndi chiwiri, ndi krusolito; achisanu ndi chitatu, ndi berulo; achisanu ndi chinai, ndi topaziyo; akhumi, akhumi ndi chimodzi, ndi huakinto; ndi krusoprazo; akhumi ndi chiwiri, ndi ametusto."*

Vesi 21: *"Ndipo zitseko khumi ndi ziwiri ndizo ngale khumi ndi ziwiri; chitseko chiri chonse pa chokha cha ngale imodzi. Ndipo khwalala la mzinda ndi la golide woyengeka, ngati mandala openyekera"*

Vumbulutso la Mkwatibwi la mzinda uwu ndi lowala ngati krustalo. Ife tonse tikudziwa kuti sipanakhalepo golide wowala ngati galasi. Koma apa, pamene muyang'ana pa mzinda, unapangidwa ndi golide weniweni, ngati galasi lowala. Kodi Yesu anawuuza chiyani mpingo uwu wa Laodikaya? *"Ndikulangiza iwe ugule kwa ine golide woyengeka ndi moto."* Kodi ichi ndi chiyani? Ndi chikhulupiriro cha oyeramtima. Ndi chimene Mulungu wabereka mu Mzimu kudutsa mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo, ndi kudutsa mu m'bado wa ku Chipangano Chakale, pamene anthu amakhulupirira ndi kugwiritsitsa pa Mulungu. Mulungu anabereka chinachake, ndipo akubwera kudziko kudzakhala pakati pa chimene Iye wabereka mu mibado iyi yonse. Inu munabwera ku mzinda uwu pamene munavomereza Mulungu ndi Mau ake. Zonse za izi zatsirizidwa mu m'bado wa muyaya, ndipo ndi zonse za uzimu, kupatula delaro.

Kodi mukutha kuona mzinda wokongola umene Yohane adawuona? Petro anaika maziko oyamba, chifukwa iye anali woyamba amene analankhula pa tsiku la Pentekosite ndipo ku Mateyu, chaputala 10:2-4, dzina lake ndiloyamba mu dongosolo la maina a atumwi. Kenako atumwi ena anayamba kuika pa maziko omwewa, ndiko kupanga maziko khumi ndi awiri. Atumwi onse khumi ndi awiri a Chiyuda anaphunzitsa chimodzimodzi.

Kodi miyala ya mtengo wapatali iyi ndi chiyani? Vumbulutso lanu ndi mwala. Kodi miyala imeneyo imapangidwa motani? Ina ya iyo imapangidwa kuchokera ku moto wochuluka. Ina imapangidwa kuchokera kukupsinjika. Zikuonetsera miyoyo imene khumi ndi awiri atumwi oyamba a chiyuda anakhala. Iwo amakhala mopsinjika ndipo amakhala mu mayesero akulu, koma iwo anaika maziko pamene iwo analalikira dongosolo lalikulu iri la chipulumutso, ndipo zikuonetseredwa apa mu maziko.

Kodi ife taona chiyani pa za mzinda? Ife taona kunja kwa iwo. Ife tikuona kuchuluka kwa malo iwo ukukhalapo. Ife tikuona kumene likulu la Mulungu liri, **koma sitinawone mkati mwa zipata ndi chimene chiri m'menemo.** Muli mtengo wa moyo ukubereka zipatso zake, ndipo ife tizipeza zimenezo ku chaputala cha makumi awiri ndi chiwiri.

Vesi 22: *"Ndipo sindinaona Kachisi momwemo; pakuti Ambuye Mulungu Wamphamvuyonse, ndi Mwanawankhosa ndiwo kachisi wache."*

Ife tikuwerenga mu vesi lachitatu la chaputala ichi kuti Kachisi wa Mulungu anali ndi anthu. Apa pa vesi 22, akuti panalibe kachisi mwa iwo. Kodi kachisi ndi chiyani tsopano? Ife, Mkwatibwi wa Khristu, ndife kachisi wa uzimu wa Mulungu. Ife timamupanga iye. Mulungu ali mwa ife, ndipo ife tiri mwa Iye.

Vesi 23: *"Ndipo pa mzinda sipafunika dzuwa, kapena mwezi wakuuwalira; pakuti ulemerero wa Mulungu uwunikira umenewu, ndipo nyali yake ndiye Mwanawankhosa."*

Mkati mwa mzinda, ngati akanati ayeze mu mamailosi, zikanakhala mamailosi masikweya 1500. Mwanawankhosa ndiye kuunika kwa mzinda. Ulemerero wa Mulungu ndi Mwanawankhosa anaunikira iwo, ndipo ife sitidzasowa dzuwa kuti iwunikire mzinda. Kodi izi zikutanthauza kuti dzuwa ndi mwezi sizidzawala? Yesaya 30 akuti, pamene Mulungu akonza vuto la anthu Ake, mwezi udzawala ngati nthawi ya usana ndipo dzuwa lidzawala ngati kuwala kwa masiku asanu ndi awiri. Dziko lidzawalira dziko lonse. Mwezi udzapitiriza kuwala. Mpando wa chifumu ukungowalira malo ozungulira mamailosi masikweya 1500. **Dziko lonse lidzasowa dzuwa ndi mwezi ku kuwala. Mu zauzimu zake, Mkwatibwi wa Khristu ndi amene akuwalira m'bado uno ndi uthenga woona wa kuwala.**

Vesi 24: *"Ndipo amitundu adzayenda mwa kuunika kwake; ndi mafumu a dziko atenga ulemerero wao kulowa nawo momwemo."*

Apa ndi pamene ine ndikufuna kuti inu mutenge vumbulutso. Mafuko adzayenda mwa mu kuwala kwa mzinda ndipo adzabweretsa kuwala ulemelerero wawo mu iwo. Kodi mafuko amenewa ndi ati? Kodi iwo anachokera kuti? Pamene ulamuliro wa mileniamu uyamba, Yesu adzayamba kuweruza anthu pa dziko lino ndi kulora ena kulowa mu mileniamu. [Mateyu 25:31-40] Iwo adzachulukana pa dziko. Pamene umuyaya uyamba, padzakhala mafuko a anthu pa dziko lonse lapansi amene sananyengedwa pamene satana anamasulidwa ku ndende mu chaputla 20. Ndi amene vesi 24 ikulankhula za iwo. Mafuko awa a wanthu adzakhala pa dziko iri ndipo adzakhala ndi moyo wamuyaya. Iwo sadzakhala mzinda. Iwo adzakhala dongosolo losiyana la oyeramtima. Mafuko awa a iwo amene apulumutsidwa adzayenda mu kuwala kwa iwo; mwakulankhula kwina iwo adzabwera ku dera iri la mailosi 1500. Iwo sadzakhala ndi matupi aulemerero monga Mkwatibwi adzakhalire, mu maonekedwe amenewo, koma Mulungu adzakhala ndi nyengo yabwino pa dziko lonse lapansi kwa iwo. Sipadzakhalanso nyanja. Anthu akhoza kudzayenda kupita ku Yerusalemu nthawi ina iriyonse kuchokera pa malo ena aliwonse pa dziko. Padzakhala njira yapamtunda kuchokera ku kontineti iriyonse. Padzakhala mitsinje ikulu ikulu ndi paradaizo wokongola pa dziko lonse. Padzakhala mitsinje ikulu ikulu ndi zina. Adzakhala paradaizo wamkulu wa Mulungu.

Vesi 25: *"Ndipo pa zipata zake sipatsekedwa konse usana, pakuti sikudzakhala usiku komweko."*

Kodi ndikuti kumene sikudzakhala usiku? Mu mzinda, koma kotsalira kwa dziko kudzalandira kuwala kwake kuchokera ku dzuwa ndi mwezi monga ziriri pano, koma mwangwiro.

Vesi 26: *"Ndipo adzatenga ulemelero ndi ulemu wa amitundu nadzalowa nao momwemo."*

Padzakhala mafuko pa dziko lonse lapansi amene adzabweretsa ulemerero wao ndi ulemu mudera iri kumene mpando wachifumu wa Mulungu idzakhazikitsidwa.

Mulungu adzapereka chinyontho ku dziko monga m'mene anachitira chigumula chisanafike, kusanayambe kumagwa mvula. Zidzakhala mwa mgwiro. Zomera zidzakhala pa dziko lonse.

Adzakhala paradaizo wa Mulungu pompano pa dziko. Ngakhale munthu, muthupi padzakhala pabwino kukhala pano. Mafuko amenewo, oyera mtima mu gawo la anthu, adzakhala ndi moyo wamuyaya. Iwo akhoza kuyendera mzinda uwu, koma sangathe kukhala gawo la iwo. Iwo adzakhala pa dziko onse lapansi, koma sadzakhala mokhazikika mu mzinda. Iwo sadzakhala gawo la mzinda. Iwo adzakhala osamalira dziko.

Vesi 27: *"Ndipo simudzalowa konse kosapatulidwa kapena iye wakuchita chonyansa ndi bodza; koma iwo okha olembedwa m'buku la moyo la Mwanawankhosa."*

Kodi zingadzatheke bwanji mu ora limenelo kubweretsa chirichonse mu mzinda chimene chiri chonyansa kapena chopanga bodza? Inu simungathe kuchita zimenezo. Izo zidzakhala za kale. **Ndipanopa pamene anthu akuyesera kubweretsa zinthu ngati zimenezo mu mzinda, koma Mulungu akuzikana izo nthawi iliyonse.** Ndi chifukwa chake Mulungu amatumiza angelo ake ndi kulekanitsa tirigu ndi nansongole. Mzinda umenewo ukupangidwa pakadali pano.

Vesi 27 imaponya anthu ambiri mu chingwe, chifukwa iwo amayesera kuika zinthu mu m'bado wa muyaya zimene zimadetsa, koma Mkwatibwi akudziwa kuti mzindawo ukupangidwa tsopano ndipo **Mulungu sadzalora chirichonse mu Mpingo Wake Woona chimene sichikhala moyo wa Umulungu mu nthawi ino.**

Mu chaputala ichi ife taona gawo lakunja la mzinda umenewo, kunja kwa mokhalamo mwa Mulungu. Ife tiri ndi zipata, maziko ndi malinga, ndi zina zotero. Kodi muli chiyani mkatimo? Mkwatibwi, mzinda umenewo wa Mulungu. Inu mumamanga makoma kuzungulira mzinda, koma khoma iri limalumikizana ndi mzinda. Ife ndi mzinda umenewo. Ife ndife Mkwatibwi. Koma kodi chitetezero chathu ndi chiyani? Kodi chikhulupiriro chathu chakhazikika pati? Ife timawerenga za akulu amenewo, ndipo chikhulupiriro chawo ndi chitsanzo kwa ife. Panali munthu dzina lake Abrahamu amene anakhulupirira Mulungu pamene chiyembekezo chonse chinatha, ndikugwiritsitsa ku Mau. Chimapereka ku moyo wanga chinachake chotsamirapo pamene ndiganiza za chimene Mulungu anachita kupyolera mwa Israeli, pamene amaika zipata ku Chipangano Chakale. Ine ndikhoza kutsamira pa zipata zimenezi, podziwa kuti maziko anaikidwa ndi atumwi khumi ndi awiri a Chiyuda a Mwanawankhosa. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHA MAKUMI AWIRI NDI CHIWIRI

Ife tikufuna timangirire mu chaputala ichi cha makumi awiri ndi chiwiri cha Chivumbulutso ndi chaputala cha makumi awiri ndi chimodzi. Mu chaputala cha makumi awiri ndi chimodzi, ife tinaona kuti Mulungu wa kumwamba akubwera ku dziko ulamuliro wa mileniamu utatha. Iye akubweretsa likulu lake, mpando wache wachifumu, ku malo ena ake. Onse amene iye wawaombola kuyambira nthawi ya Adamu, onse amene ali ndi matupi aulemerero, onse amene ali mu gawo la uzimu la oyeramtima a ulemerero ali mumalo awa, ndipo akutchedwa mzinda wa Mulungu. Tsopano tiyeni tiyambe chaputala cha makumi awiri ndi chiwiri.

Vesi 1: *"Ndipo anandionetsa mtsinje wa madzi a moyo, wonyezimira ngati krustalo, otuluka ku mpando wachifumu wa Mulungu ndi Mwanawankhosa."*

Izi zikuimirira kusefukira kwa moyo wa Mulungu mu mtima. Mzimu wa Mulungu umapatsa moyo, moyo. Ndi mtsinje wosatopa wa madzi a moyo kumene moyo umamwako ndipo

umadalitsidwa. Umatsikira kuchokera ku mpando wa chifumu wa Mulungu. Awa si madzi wamba. Palibe madzi wamba amene adzakupatsani inu moyo wamuyaya. M'munda wa Edeni, mtsinje unatuluka kuchokera ku munda kudzapereka moyo ku thupi ku moyo wathupi wa mbewu, kupereka chakudya kwa munthu wa thupi [Genisis 2:10] kwa kukhala moyo kwake ku thupi, koma pali mtsinje wa uzimu kwa mzimu waludzu wa munthu. Yesu anati ku Yohane 7:37-39- kuti kunja kwa mimba ya okhulupirira mudzatsikira mitsinje ya madzi a moyo, ndipo amenewo ndi mtundu wa madzi amene amatsikira kuchokera ku mpando wa chifumu wa Mulungu apa. Oyeramtima ali kale ndi moyo wamuyaya. Mafuko ali kale ndi moyo wamuyaya, ndipo akhoza kubwera ndi kudzamwa ndipo miyoyo yawo yadzaza ndi kukondwera. Mulungu ndi watsopano kwa iwo nthawi zonse.

Vesi 2: *"Pakati pa khwalala lache, ndi tsidya iri la mtsinje, ndi tsidya lache lija panali mtengo wa moyo wakubala zipatso khumi ndi ziwiri, ndi kupatsa zipatso zache mwezi ndi mwezi; ndipo masamba a mtengo ndiwo akuchiritsa nawo amitundu."*

Apa akuti, *"Pakati pa khwalala lache."* Ine ndikufuna inu muone kuti pali khwalala limodzi lokha mu mzinda waukulu uwu. Zikuimirira chinachake. Zikuimirira njira imodzi yak u mtengo wa moyo. Ndi njira ya ku mpando wa Mulungu. Kenako akuti, *"Ndi tsidya iri la mtsinje, ndi tsidya lache lija panali mtengo wa moyo."* Izi zikutanthauza kuti Mkwatibwi ali moyandikira mpando wa chifumu, pamene moyo wosefukira wa Mulungu ukutsikira kuchokera ku mpando wa chifumu ndipo kenako kudzera kwa oyeramtima ena, ndipo kutuluka kunka ku gawo limene kuli anthu, kusangalatsa aliyense.

Mtengo wa moyo ukubereka chipatso chake. Ife tikudziwa kuti mwa Yesu Khristu muli moyo wa muyaya. Mwa Iye muli mtengo wa moyo. Iye ali ndi ufulu wopereka moyo kwa onse amene amuvomera Iye. Koma apa, ife tikupeza kuti sizirimwa chachimuna koma mwa chachikazi, chimene chikutionetsera ife chinthu chimodzi. **Mtengo wa moyo apa ukuimirira Mkwatibwi wa Yesu Khristu pamene iye akubereka chipatso chake.** Inu mumalankhula za Mkwatibwi woonekera. Iye ali kufupi ndi mpando wachifumu wa Mulungu. Iye adzaonekera. Iye adzakhala akubereka chipatso chake pamene mafuko a dziko lapansi akubwera pansi pa chiyanjano cha Mkwatibwi wa Yesu, pansi pa maonekedwe amenewo. Ngati kumverera kulikonse kapena chirichonse chibwera pakati pa mafuko, iwo adzachiritsidwa nthawi yomweyo akangobwera pa maso pa mtengo wa moyo umenewo, Mkwatibwi wa Khristu. Ndi chikoka chimenecho ndi chiyanjano, lingaliro lirilonse loipa limene ali nalo lidzawachokera. Kumbukirani kuti mafuko awa ndi anthu a thupi.

Mtengo wa Mkwatibwi udzabereka mitundu khumi ndi iwiri ya zipatso. Kodi zipatso ndi chiyani? Kodi ndi mtundu wa zipatso za chilengedwe zimene timadya? Sichinali chipatso cha chilengedwe pa chiyambi, sichoncho? Mtengo wa moyo sunabereke chipatso zachilengedwe. Izi ndi zipatso za Mzimu zimene Akhristu akuyenera kubereka.

Tiyeni tiwerenge ku Agalatiya ndi kuona zipatso zina za Mzimu. Agalatiya 5:22-23- *"Koma chipatso cha Mzimu ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kulezamtima, chifundo, kukomamtima, chikhulupiriro, chifatso, chiletso, pokana zimenezi palibe lamulo."* Mu bukhu la Agalatiya, Paulo mtumwi kwa Amitundu akulemba za chipatso cha Mzimu pamene iye akufaniziritsa ndi Mkwatibwi wa Amitundu, koma apa Yohane akuona, osati Mkwatibwi wa Amitundu yekha, koma woomboledwa a ku Israeli. Komanso, pali zipatso zina zitatu zimene

zaonjezeredwa chifukwa cha Israeli, chimene ndi mkazi wa Mulungu. Tsopano Ayuda ndi Amitundu alumikizana palimodzi kupanga- **"Mzinda Yerusalemu Watsopano."**

Kotero, apa pali zipatso zisanu ndi zinai za mzimu zimene Mkhristu akuyenera kebereka mu nthawi ino. Mtengo wa moyo uli pano tsopano. Ndi Khristu mwa Mkwatibwi wache wa Amitundu. Mzinda umenewo ukupangidwa nthawi ino. Ife timawerenga ku Ahebri kumene akuti inu mwabwera kale ku Phiri la Zioni. Inu mwabwera kale mu mzinda wa Mulungu Wamoyo; ndipo Mulungu mwiniwake amatsika ndikukhalamo. Apa pali zipatso zisanu ndi zinai za Mzimu. Ndipo pamene tifika kumeneko tidzaberekanso zina zitatu. Ife tidzabereka zipatso khumi ndi ziwiri za Mzimu pamene Israeli akuzindikirika ngati gawo la Mzinda.

Gawo lotsiriza la vesi lachiwiri likuti, *"Ndipo masamba a mtengo ndiwo akuchiritsa nawo amitundu."* Mu mzinda wa thupi, mu malo ochezeramo, muli mithunzi m'menemo. Izi zaonetsedwa ngati mzinda wa thupi koma mu zenizeni zake simzinda wa thupi konse. Pamene Yohane anauona iwo, chirichonse chinali ngati golide, wonyezimira ngati krustalo. Masamba a mitengo anali ochiritsa kwa mafuko. Awa si masamba a chilengedwe. Chifukwa chiyani? Chifukwa kulibenso matenda a thupi. Monga timawerenga ku chaputala cha makumi awiri ndi chimodzi kuti pamene ufika ku mzinda umenewu, pamene Mulungu afika ku dziko, pamene ufumu wa Mulungu ubweretsedwa ku chochitika, sipadzakhalanso imfa, mavuto kapena matenda. Akuti zonse zakale zapita, ndipo Mulungu anati, *"Taonani ndipanga zonse zikhale zatsopano."* **Zikubwera pansi pa chiyanjano cha Mkwatibwi wa Khristu Yesu. Kodi mukudziwa kuti zimenezi zichita chinachake kwa anthu mu nthawi ino? Ndi chifukwa chake Mulungu anati osaleka kusonkhana kwanu pamodzi ndiko koposa monga momwe muona tsiku lirikuyandikira.** [Ahebri 10:25] Pali chinachake mu kusonkhana chimene mdierekezi sangathe kulowamo. Muli chikondi, chimwemwe, ndi zipatso za Mzimu.

Mafuko adzabwera ndi kukhala pansi ndi kusonkhana pansi pa masamba. Pamene anthu akhala mu malo ochezeramo kuti alankhulane, amapita kuti? Iwo amabwera ndi kukhala mu pansi pa mtengo. Pali chinachake pazokhudza mtengo pamene upereka mthunzi. Inu mukhoza kukhala pansi ndikukhala ndi chiyanjano pansi pa mtengo ndipo zimakhala bwino. Uwu ndi mtengo wa moyo, pamene ukubereka chipatso. Mkwatibwi akubereka zipatso za Yesu Khristu.

Vesi 3: *"Ndipo sipadzakhalanso temberero lirilonse; ndipo mpando wa chifumu wa Mulungu ndi mpando wa Mwanawankhosa udzakhala momwemo; ndipo akapolo ache adzatumikira Iye."*

Kodi chimene chinayambitsa themberero pa chiyambi ndi chiyani? Anali ana a Mulungu kumvetsera mdierekezi ndi kumumvera iye amene anayambitsa themberero; koma ku m'bado wa muyaya, mdierekezi ndi onse omutsatira iye adzaonongeka mu nyanja ya moto. Ana a Mulungu adzamumvera Iye ndikumusangalatsa Iye. Ambuye alemekezeke temberero lidzachoka!

Vesi 4: *"Nadzaona nkhope yache; ndipo dzina lache lidzakhala pamphumi pawo."*

Taonani apa masomphenya aYohane, panali M'modzi okhala pa mpando wa chifumu, anali Mulungu ndi Mwanawankhosa. Mau akuti, "Iwo adzaona nkhope yache, ndipo dzina lache lidzakhala pa mphumi pawo," chimene chikutanthauza kuti Mulungu ndi Mwanawankhosa sakupanga anthu awiri mu Umulungu.

Ine ndikukhulupirira kuti pali anthu ena mu nthawi ino amene amaona nkhope yache ndipo ali ndi dzina Lake pa mphumi pawo, amene ali ndi vumbulutso la chimene Yesu ali, ndi vumbulutso la chimene dzina lache liri. Ndi chifukwa chache mu nthawi ino, inu mumapita ku madzi ndikukabatizidwa mu dzina la Yesu Khristu ku kukhululukidwa kwa machimo anu. Mkwatibwi adzakhala ndi vumbulutso la chimene Yesu ali.

Vesi 5: *"Ndipo sikudzakhalanso usiku; ndipo sasowa kuunika kwa nyali, ndi kuunika kwa dzuwa; chifukwa Ambuye Mulungu adzawaunikira; ndipo adzachita ufumu ku nthawi za nthawi."*

Kodi ndi kuti kumene sikudzakhala usiku? **Mulibe usiku mu mzinda wa Mulungu pakadali pano.** Baibulo likuti Mulungu walamulira kuwala Kwake kuwale mu m'dima, ndipo m'dima sungathe kulimbana nako. Mkati mwa ufumu wa Mulungu, gawo la Mkwatibwi, Mulungu adzalekanitsa m'dima onse ku kuwala. Ife tikubwera ku nthawi imene inu mudzakhala kapena mwa Khristu kapena kunja ku m'dima. Mwa Khristu mulibe m'dima. Izi zikulankhula za mzinda pamene Mkwatibwi akukhala mu kuwala kwa iwo. Kodi mukutha kuona chimene mzinda uli? Ndi Mulungu kubwera kwa Mkwatibwi.

Tsopano, tiyeni tipite ku malo; malo a mamailosi masikweya 1500. Umenewo udzakhala mzinda waukulu, sichoncho? Palibe mzinda pa nkhope ya dziko umene uli waukulu choncho lero, koma padzakhala umodzi. Udzakhala wonyezimira ngati galasi. Zimene zikutanthauza kuti ndi dera la dziko, limene Mulungu amene ndi Mzimu wasankha kuikapo Dzina Lake ndipo ndi malo okumaniranako a oyeramtima ake a ulemerero. Mkwatibwi wa Khristu adzakhala komweko ndi onse woomboledwa a Mulungu.

Vesi lachisanu likuti, iwo sasowanso nyali, kapena kuwala kwa dzuwa. Kodi zikutanthauza kuti dzuwa lidzaleka kuwala? Ayi. Izi zikukamba za dera lapadera la dziko, ndipo m'menemo ndi mkati mwa mzinda. Kodi inu mumalowa bwanji mu mzinda? Inu mumalowa mu iwo povomereza Yesu Khristu. Inu muli mu mzinda pakadali pano, koma malo ake ndi kumene Mulungu adzasuntha mpando Wache wachifumu, ndipo kuwala kudzatsikira kuchokera ku mpando wa chifumu. Mtsinje wa madzi, chimene ndi kutsikira kwa uzimu kwa Mulungu, kukutsikira kuchokera ku mpando wa chifumu ndipo kuwala kudzawalira. Palibe m'dima umene ungalowe mu chiyanjano cha Mulungu, pamene chiyanjano chikhala changwiro monga chinaliri mu masiku oyamba.

Mu bukhu la Machitidwe, chisomo chachikulu chinali mu mpingo. Pamene m'dima pang'ono unayesera kulowa kudzera mwa Anania ndi Safira, Mulungu anawadula iwo. Palibe m'dima umene ungalowe mu mzinda uwu. Iwo sadzasowa dzuwa. Chimene Mulungu ndi Mwanawankhosa amachita apa ku mzinda uwu, dzuwa ndi mwezi zimachita ku dziko ndi anthu ku thupi. Chimene chimachitika ndi chakuti kuwala kumayenda mbali iriyonse. Chimene kuwala kwa Mulungu kumachita kwa mzinda kuchokera ku mpando wa chifumu, dzuwa ndi mwezi zimachita ku dziko lonse. [Yesaya 30:26] Sipadzakhala usiku mu mzinda. Iwo sadzasowa dzuwa. Taonani kuti Mkwatibwi adakali pa dziko. Padakali anthu pa dziko. Mzindawo umangotenga ka gawo kochepa ka dziko, koma anthu, mafuko, akukhala pa dziko lonse la pansi. Mwakanthawi kanthawi adzidzabwera mu mzinda ndi kubweretsa ulemerero wawo mu iwo.

Ine ndikuchita ndi dera, komanso mpingo. Mafuko adzabwera kudzera pa zipata za mu mzinda; ogonjetsa adzatero. Zikutanthauza kuti pamene adzakhala akuyandikira dera limeneli, ngakhale dera lakunja la ilo, kuti iwo adzazindikira chimene Mulungu anachita ndi pfuko la Israeli poika zipata , ndipo adzazindikira chimene Mulungu wachita kupyolera mwa atumwi khumi ndi awiri poika maziko a linga. Iwo adzazindikira Ayuda ophedwa ndi Hitler, ndi onse ophedwa mu nthawi ya chisautso, ndi oyeramtima aku chisautso, ndi ena otero, pamene zikulumikizana palimodzi ndi kupanga mzinda umodzi. Pamene Yohane anaona mzinda

ukubwera ukutsika, zonse zinali m'malo mwake. Mafuko a anthu adzakhala ndi vumbulutso. Iwo amene agonjetsa adzalowa kudutsa mu zipata kulowa mu mzinda. **Inu mukuyenera kukhala ndi vumbulutso tsopano kuti mukalowe mu mzinda kudzera pa chipata. Ife tikudziwa chimene zipata ziri, kodi sichoncho?**

Vesi 6: *"Ndipo anati kwa ine, Mau awa ali okhulupirika ndi woona; ndipo Ambuye, Mulungu wa mizimu ya aneneri, anatuma mngelo wache kumuonetsera akapolo ache zimene ziyenera kuchitika msanga."* Zolankhula izi ndi zoona, koma zimatengera vumbulutso la izo. Ine ndikufuna ndikuonetsereni inu m'mene Mulungu anayamba kuzifanizitsira izi ndi kukuonetserani ngakhale malo ake ku Chipangano Chakale. Ngati ukanakhala m'ndandanda wa mapiri mudera iri la ma mailosi 1500, ndiye kuti simukanatha kuona mpando wachifumu wa Mulungu. Koma nthawi yomweyo inu mukangolowa mu mzinda uwu, mu kuwala uku, mudera limene ana a Mulungu ndi woomboledwa ali mu nthawi ino, inu mukhoza kuona mpando wa Mulungu.

Mu nthawi imene Mulungu akulenga kumwamba kwatsopano ndi dziko latsopano, Mulungu adzasanja mapiri bwinobwino, ndi mpando wa chifumu wa Mulungu udzakhazikitsidwa pa mwamba pa mapiri.

Chirichonse chimene Mulungu akuchita mu umuyaya, Iye anayamba kupereka vumbulutso kale mbuyomo pansi pa akuru komanso mu nthawi ya Davide. Baibulo limakamba za mzinda Yerusalemu Watsopano, malo ake, pokhala pake. Likukamba za phiri. Akuti, *"Yehova ndiye wamkuru, ayenera kulemekezekadi, M'mzinda wa Mulungu wathu, m'phiri lache loyera."* Akuyamba kukamba za mzinda wa Mulungu ndi mapiri a Mulungu. Masalimo anati, *"Chikhalidwe chake nchokoma."* [Masalimo 48:1-3]

Tiyeni tiwerenge Yesaya 2:2- *"Ndipo padzakhala masiku otsiriza, kuti phiri la nyumba ya Yehova lidzakhazikika pa msonga ya mapiri, ndipo lidzakwezedwa pamwamba pa zitunda; mitundu yonse idzasonkhana kumeneko."* Ine ndikukuonetserani inu maonekedwe a malo kumene Mulungu akutsikira mu m'bado uwu wamuyaya. Yesaya 2:3- *"Ndipo anthu ambiri adzanka, nati, Tiyeni tikwere kunka ku phiri la Yehova, ku nyumba ya Mulungu wa Yakobo; ndipo Iye adzatiphunzitsa za njira zache, ndipo tidzayenda mu mayendedwe ache; chifukwa mu m'Ziyoni mudzatuluka chilamulo, ndi mau a Yehova kuchokera mu Yerusalemu."* Mfundo imene ndikufuna inu muone ndi iyi, *"Tiyeni tikwere kunka ku phiri la Yehova."*

Mneneri Yesaya samayang'ana mileniamu yokha, koma amayang'ana kupyola iyo pamene amalankhula mau a uneneri. Izi zikuonetsera malowo. Ngati phiri sirinapangidwe bwino pa nthawi iyi, Mulungu adzalipanganso bwino mu nthawi imeneyo kuti kuwala kwake kukawale. Mulungu akubwera pa dziko lino ndipo adzakhala pa malo apamwamba pa nkhope ya dziko. Kuwala kochokera ku mpando wachifumu kudzawalira mbali iriyonse mudera iri la ma mailosi 1500.

Mafuko amenewo a thupi adzabwera ndi kukhala ndi chiyanjano pansi pa mtengo wa moyo. Njira za Mulungu zidzakhalabe zatsopano kwa iwo. Mavumbulutso a tsopano a Mulungu adzaonekera pamene akubwera ndi kukhala pansi pa chiyanjano, ndi kudya zipatso za Mzimu; ndi masamba a mtengo ndi a machiritso a mafuko.

Tiyeni tiyambe kuchita ndi zina za zinthu zokhudza mpingo, gawo la uzimu la mzinda, ndipo ndikukhulupirira Ambuye kuti sipakhala chirichonse mu Bukhu iri la Chivumbulutso chimene

simukuchiona bwino, “monga kuwala kwake kuli kowala ngati krustalo,” ndi chifukwa chache mukhoza kuona izi.

Mu chaputala chachitatu cha Akorinto woyamba, Paulo akuyamba kulankhula. 1 Akorinto 3:10-11- *“Monga mwa chisomo cha Mulungu chidapatsidwa kwa ine, ngati mwini mamangidwe waluso, ndinaika maziko, koma wina angamangepo. Koma yense ayang’anire umo amangira pamenepo. Pakuti palibe munthu akhoza kuika maziko ena, koma amene aikidwako, ndiwo Yesu Khristu.”* Mu chaputala cha makumi awiri ndi chimodzi cha Chivumbulutso ife tikuwerenga za maziko, *maziko khumi ndi awiri.* Apa, Paulo akulankhula, *“Ine ndaika maziko.”* Uthenga wa Paulo unabwera m’bado wa Ayuda utatha; koma palibe mzinda ngakhale umodzi wa Ayuda ndi wina wa Amitundu, ndi zina zotero. Pali mzinda umodzi. Ndi chimene Paulo anachiona.

Taonani chimene kachisi wa Mulungu ali. 1 Akorinto 3:16- *“Kodi simudziwa kuti muli kachisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu?”* Kodi kachisi wa Mulungu ndi chiyani? Inu ndinu kachisi wa Mulungu. Mzimu wa Mulungu *agonera mwa inu.* 1 Akorinto 3:17- *“Ngati wina aononga kachisi wa Mulungu, ameneyo Mulungu adzamuononga; pakuti kachisi wa Mulungu ali wopatulika; ameneyo ndi inu.”* Kodi mukuona chimene kachisi wa Mulungu ali? Kodi mukuona chimene chikutsika? Ndi Mulungu kudzoza kachisi wake. Ife ndife kachisi wa Mulungu.

Tiyeni titsegule ku Aefeso. Ine ndikufuna ndikuonetsereni chinachake chokhudza maziko. Apa Paulo anaika maziko a kachisi. Zonse zikuyenera kulumikizana palimodzi kupanga kachisi.

Ine ndikuonetserani m’mene zikugwirizanirana. Maziko a linga akumangirizana palimodzi ndi maziko a mzinda. Izi zikukubwera ku mzinda wa uzimu, ndipo pali gawo limodzi limene ine sindikufuna kuti muphonye. Taonani bwinobwino malankhulidwe a lemba lotsatira. Aefeso 2:20- *“Omangika pa maziko a atumwi ndi aneneri, pali Kristu Yesu mwini, mwala pa ngodya.”* **Taonani maziko. OSATI maziko ambiri.**

Taonani bwinobwino pamene tikuyang’ana za vumbulutso la Paulo la mzinda uwu, kapena kachisi wa Mulungu, ndi kumuyerekeza iye ndi masomphenya a Yohane. Paulo anati, *“Omangika pa maziko,”* Maziko AMODZI. Yohane anati linga linali ndi *maziko* khumi ndi awiri otchulidwa mwa maina khumi ndi awiri a atumwi a Mwanawankhosa. Paulo anati, **“Ine”** ndaika maziko [1 Akorinto 3:10], ndipo ife tamangidwa pa maziko a atumwi aku Chipangano Chatsopano ndi aneneri aku Chipangano Chakale. Kodi tiri nako kutsutsana apa? Mwantheradi ayi. **Chimene Yohane anachiona ngati zipata zotchulidwa mwa mafuko khumi ndi awiri a atumwi, maziko anatchulidwa mwa maina khumi ndi awiri a atumwi a Mwanawankhosa, Paulo anaona ngati aneneri aku Chipangano Chakale ndi atumwi a Chiyuda aku Chipangano Chatsopano. Amuna awiri onsewa anaona chinthu chimodzimodzi.** Paulo anatenga chimene aneneri aku Chipangano Chakale ndi chimene atumwi aku Chipangano Chatsopano ananena ndi kuziika izo mu dongosolo la Mulungu kwa ife. Zimatengera zonse malemba a ku Chipangano Chakale ndi Chipangano Chatsopano kukatsiriza dongosolo la Mulungu. Ku Chivumbulutso chaputala 21 ndi 22, Yohane akuona chinthu chonsechi chikuikidwa pamodzi ndipo angelo, kapena mkuru, anazitcha izo Mzinda Woyera, Yerusalemu Watsopano, mkazi wa Mwanawankhosa, **zonse ndi zauzimu,** kupatula deralo.

Ayuda anabwera mofulumira ndipo anaika maziko a linga la mzinda. Iwo anaika maziko polalikira uthenga umene analalikira zaka zochepa zoyambirira Pentekosite atatha.

Ine ndikufuna ndikuonetsereni inu m’mene Paulo anafikira ndi kusonkhanitsa pamodzi, chirichonse cha zoonadi zimene atumwi analalikira. Aefeso 2:20, akuti Yesu Khristu mwiniwake

ndi mwala wa ngodya. Paulo anafikira ku mauthenga anai kumene kwalembedwa zochitika za Yesu, ndi kuzilumikiza zonse izi mu maziko ndi kupanga maziko a mzinda ndi kulumikiza palimodzi linga. Zikuonetsera kulumikizana pakati pa Ayuda ndi Amitundu. Maziko aikidwa, ndipo Paulo anafikira ndi kutenga chiphunzitso cha wina aliyense wa atumwi. Kwenikweni onse a iwo analankhula chinthu chimodzi. Kodi Paulo analankhula chiyani pa za ubatizo wa m'madzi ku chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chinai cha Machitidwe. Iye anafikira ndi kukatenga chiphunzitso cha Petro pa tsiku la Pentekosite. Iye analumiza izo mu kuika maziko. Iye anatenga maziko onse awa a linga ndi kupanga maziko a Mkwatibwi wa Khristu. Iye anaphwanya khoma lotchinga la pakati logawa Ayuda ndi Amitundu. [Aefeso 2:14]

Tsopano, tiyeni tiwerenge Aefeso 2:20-22, chifukwa ine ndikufuna kuti muone mau oti "maziko," maziko amodzi. *"Omangika pa maziko a atumwi ndi aneneri, pali Khristu Yesu mwini, mwala wa pangodya, mwa Iye chimango chonse, cholumikika pamodzi bwino, chikula, chikhale kachisi wopatulika mwa Ambuye; chimene inunso munamangidwamo pamodzi, mukhale chokhalamo Mulungu mwa Mzimu."* Kodi mokhalamo mwa Mulungu muli kuti? Ndi mwa ife, ndipo ife tamangidwa pa maziko a atumwi ndi aneneri. Paulo anali wolankhula wamkuru amene anabwera m'bado wa Ayuda utatha. Atumwi khumi ndi awiri analalikira uthenga zaka zoyambirira Pentekosite atatha kudzaika *maziko* a linga. Ndipo Paulo anabwera ndi kutenga chiphunzitso chawo ndi kupanga *maziko* a kachisi ndi kubweretsa uthenga wapadera ku gawo la Amitundu ku mzinda. [Aroma 11:13] Paulo anati, **"Ine ndine mtumwi kwa inu Amitundu."** Tsopano Petro, ku mbali ina, anali mtumwi wa kwa Ayuda, ndipo anadziwa kuti mzindawo unali wauzimu monga zapangidwa kumveka bwino ndi 1 Petro 2:3-9.

Kumbukirani m'mene tinazibweretsera mu phunziro lathu la chaputala cha makumi awiri ndi chimodzi kuti Paulo ananena mu chaputala cha chitatu cha Aroma, *"Kodi chipindulanji kukhala mu Yuda?"* Iye anati, *"Zambiri monse monse: choyamba kuti mau a Mulungu anaperekedwa kwa iwo."* Zinaperekedwa kwa iwo kuti Mulungu ndi Mulungu m'modzi, chikhulupiriro chimodzi, ndi Ambuye, ndi zina zotero. Iwo anagwira choonadi ichi pakati pa zipembedzo zambiri za chikunja.

Pofuna kukuonetserani pang'ono pa chimene Paulo anaikamonso, tiyeni tione ku Aefeso 4. Ichi chikuonetserani utumiki umene Paulo anaika [kuima m'malo] mu malo ake oyenera. Paulo anafikira ndikutenga chiphunzitso cha chiyuda ndi kuchiika molondora kwa Mkwatibwi wa Amitundu. Pamene m'bado wa Amitundu umatha, iye anatenga Mau amene Mulungu anaulura kwa iye ndi kuika maziko amenewo amene anaphatikiza zambiri za zomwezo zimene Petro anaphunzitsa; monga Mulungu m'modzi, ndi ubatizo wa m'madzi mu dzina la Yesu Khristu monga zalembedwera mu Mau. [Machitidwe 2:38] Iye anapanga uthenga umodzi kuchokera kwa iwo kwa Mkwatibwi wa Khristu, kachisi wa Mulungu, kuti amangidwirepo. Nkhani ndi yakuti, Paulo ndi amene anatenga maudindo asanu awa a utumiki ndi kuwaika iwo kwa Mkwatibwi wa Amitundu.

Iri ndi dongosolo lolondora la utumiki wa ku Chipangano Chatsopano monga zinaikidwira ndi Paulo Woyera. Aefeso 4:11-16- *"Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi ena aneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi."* [Taonani Paulo akuika maziko ndi kuika utumiki mu m'mene Mulungu akhoza kugwira ntchito kupyolera mwa iwo]. *"Kuti akonzere oyera mtima ku ntchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu; kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa*

chikhulupiriro, ndi wa chizindikiritso cha Mwana wa Mulungu, kwa munthu wa ngwiro, ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Khristu. Kuti tisakhalenso makanda, ogwedezeka gwedezeka , natengeka tengeka ndi mphepo yonse ya chiphunzitso, ndi tsenga la anthu, ndi kuchenjera kutsata chinyengo chakusocheretsa, koma ndi kuchita zoona mwa chikondi tikakule mu zinthu zonse, kufikira Iye amene ali mutu ndiye Khristu; kuchokera mwa Iye thupi lonse, lokowanidwa ndi kulumikizidwa pamodzi, pothandizanapo mfundo yonse, monga mwa kuchititsa kwa chiwalo chonse pa muyeso wache, lichita malankhulidwe a thupi, kufikira chimango chache mwa chikondi." Aka ndi kakonzedwe ka mzinda. **Pamene tifika ku chidzalo cha thunthu la thupi la Khristu, ndiye timapanga mzinda wa mkati, Mkwatibwi amene amabereka chipatso. Apa pali chidzalo cha thupi.**

Mkazi wa Mwanawankhosa wazikongoletsa ngati mkwatibwi kwa mamuna wake ndi chidzalo cha thunthu la mamuna Yesu Khristu. Ndi thupi loikidwa kwathunthu pa maziko a atumwi, ndi aneneri, Yesu Khristu pokhala mwala wa pa ngodya. Petro anachibweretsa ichi. Iye anaona zinthu izi, koma zimatengera Paulo kuziika palimodzi pamene iye amatenga maziko ndi kuwaphatikiza pamodzi kupanga maziko a Mkwatibwi wa Khristu. Taonani, pamene tiona Mkwatibwi, mzinda uwu ndi onse Ayuda ndi Amitundu. Ku Chipangano Chakale, Israeli anali Mkwatibwi wa Mulungu. Ku Chipangano Chatsopano, Amitundu ndi Mkwatibwi wa Yesu Khristu, koma apa pa Chivumbulutso, chaputala 22:3, akukamba za mpando umodzi wa chifumu, ndi m'modzi okhala pa mpando wa chifumu, ndipo akutchedwa Mulungu ndi Mwanawankhosa; osasiyanitsanso pakati pa Atate ndi Mwana. Ife tikuona M'modzi wokhala pa mpando wachifumu mu Mzinda. Zonse zikubwera palimodzi pano mu m'bado wa muyaya. Mulungu m'modzi, ndi mkazi m'modzi, wopangidwa mwa mafuko onse. Maziko onse aphatikizidwa apa mu chiphunzitso cha Paulo. Pamene Paulo anatsiriza kulalikira Uthenga, zonse zimene Petro analalikira, zimene Yakobo analalikira, zimene Yohane analalikira, zimene Yuda analalikira, anazifikira ndikuphatikiza zoonadi izi ndikuzibweretsa palimodzi kupanga thunthu la chidzalo la munthu Khristu Yesu. Mu zauzimu zake, kumeneko ndi kulumikiza khoma ku mzinda onse. Ndi kulumikiza maziko kuti pasakhale kulekana pa iwo. Ife talowa kale mu zipata za mzinda umenewo. Ife tachokera kale kutali. Zinatengera m'modzi [Paulo] khumi ndi awiri atapita, kukatenga timapisi ndikutiphatikiza palimodzi bwinobwino kupanga gawo iri la mzinda.

Vesi 7: *"Ndipo taonani, ndidza msanga. Wodala iye amene asunga mau a chinenero cha bukhu iri."*

Vesi 8: *"Ndipo ine Yohane ndine wakumva ndi wakupenya izi. Ndipo pamene ndinamva ndi kupenya, ndinagwa pansi kulambira pa mapazi a mngelo wakundionetsa izo."*

Vesi 9: *"Ndipo ananena kwa ine, Tapenya, usachite; ndine kapolo mnzako, ndi mzawo wa abale ako aneneri, ndi wa iwo akusunga mau a bukhu iri, lambira Mulungu."*

Kodi mngelo uyu ndi ndani amene Yohane anagwa kuti amulambire? Mu chaputala cha Chivumbulutso, wina anabwera ndi kuyamba kulankhula ndi Yohane. Munthu yemweyu akulankhula ndi Yohane mu chaputala cha chisanu ndi chiwiri. Ndipo mu chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chinai, tikuona kulankhula kofafanaku kwa Yohane, ndipo Yohane akugwa pansi ndi kulambira iye. Iye anati, *"Tapenya, usachite; ndine kapolo mnzako."* Ena ayerekeza iye kukhala m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri a pansi pano a mu m'bado wa mpingo, chifukwa m'modzi wa angelo asanu ndi awiri anamutenga iye mu mzimu pamene iye anaona mzinda, koma pamene tiwerenga Chivumbulutso 22:9 zikutionetsera ife poyera. Akuti, *"Ndine kapolo mnzako, ndi mzawo wa abale ako aneneri."* Ife tikudziwa kuti angelo awa asanu ndi awiri ndi angelo auzimu. Uyu ndi m'modzi mwa akuru makumi awiri mphambu zinai. Ndi yemweyo

amene anali mu chaputala cha chisanu, chachisanu ndi chiwiri, komanso ku chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chinai cha Chivumbulutso. Si m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri auzimu. Ndi munthu, ndi mneneri, ndi m'modzi mwa akapolo. Ndi m'modzi mwa akuru makumi awiri mphambu zinai amene Yohane anawaona pamene iye anatengwedwa mu chaputala chachinai cha Chivumbulutso. Mngelo wa uzimu anamutenga Yohane mu uzimu kuti akathe kuona mzinda, koma m'modzi amene anafotokozera iye anali m'modzi mwa akuru. Ndi chifukwa cha kupezeka kwa m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri kuti Yohane anagwa pansi kumulambira, potengedwa ndi kukhalapo kwake koma osazindikira kuti anali mkuru kulankhula ndi iye mpakana kupezeka kwa mngelo kutachoka. Kenako Yohane anaona bwinobwino amene amalankhula ndi iye.

Vesi 10: *"Ndipo ananena ndi ine, usasindikiza chizindikiro mau a chinenero cha bukhu iri; pakuti nthawi yayandikira."* [*"Nthawi yayandikira"* ndi pamene zikumasuliridwa, ndipo ndi nthawi ino.]

Vesi 11: *"Iye wakukhala osalungama achitebe zosalungama; ndi munthu wonyansa akhalebe wonyansa; ndi iye wakukhala wolungama achitebe zolungama; ndi iye amene ali woyera akhalebe woyeretsedwa."*

Tsopano ndi nthawi imene mukhoza kuona lemba ili kukwaniritsidwa. Palibe kulapa kochuluka kumene kukuchitika.

Vesi 12: *"Taonani ndidza msanga; ndipo mphotho yanga ndiri nayo yakupatsa yense monga mwa ntchito yache."*

Vesi 13: *"Ine ndine Alefa ndi Omega, woyamba ndi wotsiriza, chiyambi ndi chitsiriziro."* [Izi zikuonetsera umulungu.]

Vesi 14: *"Odala iwo amene atsuka miinjiro yawo, kuti akakhale nawo ulamuliro pa mtengo wa moyo, ndi kuti akalowe mu mzinda pazipata."*

Ndi zimene takhala tikulemba za izo. Iwo akhoza kusangalala ndi kupezeka kwa moyo wotsikira nthawi zonse wa Mulungu. Kodi zikutanthauza chiyani pamene akuti, *"Ndi kuti alowe mu mzinda pa zipata"* Zikutanthauza kukhala ndi vumbulutso la Mulungu m'modzi. Kodi inu munalowa mu mzinda kudutsa mu zipata? Kodi zipata ndi chiyani? Ife tinagwira lemba pamene Paulo anati kwa Israeli kunaperekedwa malamulo a Mulungu. Zimenezo ndiye zipata. Zikubwera ku vumbulutso la Mulungu monga zabweretsedwera kupyolera mwa Israeli, kupyolera mwa atumwi khumi ndi awiri, kupyolera mwa Paulo woyera, ndi ku thupi la Khristu mu nthawi ino. Inu mulowe mu zipata. Mu zenizeni, ndi pamene maiko alowa mu Yerusalemu ndi kufika ku malo amenewo. **Mafuko a anthu athupi adzakhala ndi vumbulutso la chimene Mulungu anachita kupyolera mwa pfuko la thupi Israeli.**

Vesi 15: *"Kunja kuli agaru ndi anyanga, ndi achigololo, ndi ambanda, ndi opembedza mafano, ndi yense wakukonda bodza ndi kulichita."*

Funso linafunsidwa, "Pamene m'bado wa muyaya uyamba ndipo mzinda utsika, kudzatheka bwanji osakhala achigololo, agaru, amatsenga ndi ena otero, kunja kwa mzinda?" Ndi funso labwino kwambiri. Tiyeni tirione motere. Poti tikuona chimene mzinda uli, ife tikhoza kuyankha funso limenelo. Mzinda ukupangidwa tsopano, ndipo wakhala nthawi yonseyi. Inu mumalowa mu mzinda kapena mumazindikirika ndi chivundi chimene chiripo. Palibe chimodzi cha icho chidzalowa mu Mkwatulo pamene uchitika. Mzindawo ndi Mkwatibwi. Paulo anati mwafika ku Phiri la Zioni. Inu mumachita zimenezo mu m'bado uno.

Popanda mzinda *lero* kuli agaru, achigololo, ndi anyanga, ndi ena otero. Koma iwo sadzakhala kunja kwa mzinda mu m'bado uwu wa muyaya, chifukwa sipadzakhala aliyense wazimenezo, nthawi!

Chikatha chiweruzo cha mpando woyera wachifumu, m'bado wa muyaya ukuyamba. Yesu akuweruza chirichonse chimene sichiri choyenera kukhala ndi moyo wamuyaya ndipo chidzaponyedwa mu nyanja ya moto. Sipadzakhala wina aliyense mu m'bado wa muyaya amene ali wachigololo, wakupha, wopembedza mafano, kapena okonda ndi kupanga mabodza. Choncho, zikuyenera kuchita ndi m'bado uwu umene tikukhala tsopano. Kunja kwa mzinda mu m'bado umene tikukhalawu kuli achigololo, aziwerewere, ndi onse onenedwa apa. Sizikutanthauza kuti kudzakhala aliyense kumeneko. Sikudzakhala aliyense. Mau akuyenera kuyenda mu kupitirira. Ngati titaika anthu amene ali achigololo, akupha, ndi opembedza mafano, ndiye tikuononga chithunzi cha Mau onse a Mulungu. Ife sitingachite zimenezo.

Vesi 16: *"Ine Yesu ndatuma mngelo wanga kukuchitirani umboni za izi m'Mpingo. Ine ndine muzu ndi mbadwa ya Davide, nyenyezi yonyezimira ya nthanda."*

Vesi 16 ikutionetsera ife kuti Yesu akufuna Mpingo udziwe zinthu izi zimene inu mwakhala mukuwerenga kuchokera ku bukhu iri, makamaka Mkwatibwi wa Khristu mu nthawi ino yotsiriza, kotero adzakhala okonzeka pamene Iye abwera kwa iye. **Ndi chifukwa chake ine ndikulemba bukhu iri.**

Yesu anati, *"Ine ndine muzu ndi mbadwa ya Davide."* Paulo anafotokoza bwino kulankhula kumeneko bwinobwino ku Akolose 1:17- *"Ndipo Iye* [Yesu] *ali woyamba wa zonse, ndipo zonse zimagwirizana pamodzi mwa Iye."* Komanso, Yesu anawauza Ayuda osakhulupirira [Yohane 8:58] kuti *"Abrahamu asanakhale Ine ndinali."*

Ku 2 Timoteo 2:8 Paulo anati, *"Kumbukira Yesu Khristu, anauka kwa akufa, wochokera ku mbewu ya Davide, monga mwa uthenga wabwino wanga."* Iye anali mbewu ya Davide, chifukwa anabwera mu mbumba ya Davide [Mateyu 1:1], ichi chinali ku mbali ya mai Wake.

"Nyenyezi yonyezimira ya nthanda," ya vesi 16 ndi *"Nyenyezi ya tsiku,"* ya 2 Petro 1:19; *"dzuwa la chilungamo,"* ya ku Malaki 4:2; ndi *"Mngelo Wamkuru,"* wa ku Chivumbulutso 10, zikutanthauza chinthu chimodzi. Ndi Khristu kubweranso ku dziko mu maonekedwe a mngelo mu tsiku lotsiriza.

Vesi 17: *"Ndipo Mzimu ndi mkwatibwi anena, Idzani. Ndipo wakumva anene, Idzani. Ndipo wakumva ludzu adze; iye wofuna, atenge madzi amoyo kwaulere."* [Madzi amoyo ameneyo alipo tsopano. Iye wofuna, akhoza kubwera ndi kudzamwa. Vesi 17 ikudzifotokoza yokha.]

Vesi 18: *"Ndichita umboni kwa munthu aliyense wakumva mau a chinenero cha bukhu iri, Munthu akaonjeza pa awa, adzamuonjezera Mulungu miriri yolembedwa m'bukhumi."*

Vesi 19: *"Ndipo aliyense akachotsako pa mau a bukhu la chinenero ichi, Mulungu adzamuchotsera gawo lache pa mtengo wa moyo, ndi mzinda woyerawo, ndi pa izi zinalembedwa m'bukhumi."*

Taonani m'mene ziriri zofunika kukhala mu Mau, musaonjezere kapena kuchotsera; **mungovomereza Mau ndi kumasulira monga Mulungu akupatsirani inu.**

Inu simungathe kuchotsako ku mzinda, kapena kuonjezerako. Ndi kudziwidwiratu. Zonse zatha. Banja lonse la Mulungu liri m'menemo. Bukhu latsegulidwa.

Pamene ndikulemba izi, Ine ndikuzindikira kuti chimene Yohane anaona sichinabwere ku chidzalo pano, ndipo vesi 18 ndi 19 ndi machenjezo kwa ife kuti tiyende moyenera mu malonjezano akulu awa.

Kukhala gawo mu bukhu la moyo, zikutanthauza kuti mukuyenda mu kuwala kwa Mulungu mu nthawi ino, ndipo ndinu gawo la mzinda. Zikutanthauza kuti dzina lanu liri mu bukhu chifukwa muli ndi moyo wa bukhu. Inde tikudziwa kuti Mulungu alibe bukhu lenileni la maina, ziri mu malingaliro ake. Iye akudziwa chitsiriziro kuchokera kuchiyambi. [Machitidwe 15:18] Choncho khalani mu malingaliro Ake [bukhu] **pokhala mu choonadi chake chimene chiripo.**

Vesi 20: *"Iye wakuchitira umboni izi, anena, Indetu; ndidza msanga. Amen; idzani, Ambuye Yesu."*

Taonani, "Iye wakuchitira umboni izi, anena, *"Indetu, ndidza msanga."* Ndi Yesu amene anachitira umboni. Iye akubwera posachedwa, kodi inu mwakonzeka kukumana naye? Ngati sichoncho, Ine ndikupemphera mumuvomereze Iye tsopano. Titsirize bukhu ndi iri ndi Mau ake a Yohane.

Vesi 21: "*Chisomo cha Ambuye Yesu chikhale ndi oyera mtima onse. Amen."*